

# MOMWE MPHUNGU IKASULIRA



Tiyeni ife tikhale chiimire mphindi yokha ku pemphero.

<sup>2</sup> Misonkhano yonse yapita iyi, nthawizonse ikungondibwerera ine. Mwanjirayina, pamene ife tipezana wina ndi mzake ndi kuphunzira kudziwana, bwanji, ndipo tikangoyamba kuti tizicheza, ndiye imakhala nthawi yoti tizipita kwinakwakenso. Izo nthawizonse zimandipatsa ine kumverera kwina kwachisoni pang'ono. Koma ndikayang'ana mtsogolo, ine ndikuyembekezera tsiku limene ife tonse titi tidzakomane kachiwiri, ndipo ife tidzakakhala mu malo, mwinamwake, ngati Yesu ati adze tisanakomane pa dziko lapansi kachiwiri, komwe ife ndi pang'ono pomwe, sitidzasiyana konse.

<sup>3</sup> Ine ndikudadwa ndi angati akufuna kuti akumbukiridwe kwa Mulungu, madzulo ano, pamene ife tikukweza manja athu mu pemphero? Ambuye akudalitseni inu.

Tiweramitse mitu yathu kwa mphindi yokha.

<sup>4</sup> Mulungu Wamphamvuzonse, Mlengi wa miyamba ndi dziko lapansi, ndi Mwini wa Moyo wosatha, ndi Wopereka mphatso yabwino iliyonse, ife tikudza mu mithunzi ya chifundo Chanu, mwa pemphero, kupyolera mu Dzina la Yesu, Mwana Wanu, kuti tipereke kwa Inu mathokoza athu chifukwa cha msonkhano waukulu uwu waku Tusa, pa chimene iwo watanthauza kwa ife, malo mu mtima mwathu amene ife sitidzawaiwala konse anthu abwino awa. Ngakhale, Mzimu Wanu Woyera uli mwa iwowo, chiyanjano chake chomwe chakhala chiri: kukhudza pang'ono kwa Kumwamba mu miyoyo yathu, chotichitikira chomwe ife sitidzakhoza konse kuchiyiwala. Ife tikupemphera, Atate, kuti Mzimu Wanu nthawizonse uzikhala uli mwa anthu awa. Mulole, kuchokera ku chofunikira cha kusunkhana kwakung'ono uku, chipangitse chitsitsimutso kuti chifalikire mu mpingo uliwonse kudutsa mdziko lonseli. Mulole zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa zikwaniritsidwe. Ife tikupemphera, Ambuye, kuti Inu mupereke zinthu izi.

<sup>5</sup> Zaikidwa apa pa desiki ili, madzulo ano, ndi mipango ndi zidutswa zazing'ono za nsalu zomwe zikupita kwa odwala ndi osautsika. Mulungu Wamphamvuzonse, ine ndikukupemphani Inu, mu Dzina la Yesu, kuti yense yemwe izi ziti zikamukhudze, yemwe akudwala, mulole iwo akachiritsidwe; si pemphero langa lokha, Atate, koma pemphero la moyankhuliramo mwamukulu umu modzaza ndi Akhristu, madzulo ano. Ife tikulipereka ilo ndi chigwirizano chimodzi, chifukwa cha iwo omwe ali osowa.

<sup>6</sup> Ambuye, ife tikupemphera kuti Inu mutidalitse ife mu zochitika zotsatira za tsiku lino. Ife tikuipempherera mipingo,

usikuuno. Mulole kuti kukangokhala ulemerero ndi chimwemwe chosasimbika mu mpingo uliwonse. Tipatseni ife kutsanulira kwakukulu kwa Kukhalapo Kwanu, madzulo ano. Mulole Mzimu Woyera ubwere mu Mawu, ndipo mulole Mawu akhale mu mnofu wathu ndipo adzakhale pano ndi ife madzulo ano. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

Inu mukhoza kukhala.

<sup>7</sup> Kwa mtumiki wina aliyense, kwa ogwira ntchito onse, wosamalira pa malo, ndi kwa othandizira, ndi onse; kwa inemwini ndi gulu langa: M'bale David, M'bale Roy, Billy Paul, Loyce, M'bale Fred Sothmann, M'bale Jim Maguire, M'bale Gene, ndi Leo, ife tonse tikufuna kuti tikuthokozeni inu nonse chifukwa cha chifundo chanu, ndi zomwe inu mwatanthauza kwa ife mu msonkhano uno. Inu ndithudi mwakhala abwino kwambiri. Kulemekeza kotero ndi chikondi zomwe ife tazisonkhanitsa mu mitima yathu, kwa inu, izo sizidzafutidwa konse. Ndi zosafutika. Ndipo ife tikudalira kuti Mulungu akupatsani inu zopambana, zochuluka pamwamba pa zonse zomwe inu mungakhoze konse kuziganizira kapena kuzipempha. Mulole Mulungu apereke izo kwa inu mwa kulemera kwa chisomo cha Mwana Wake, Yesu Khristu.

<sup>8</sup> M'bale Tommy Osborn, ali muno mu msonkhano. Ambuye Mulungu akhale ndi M'bale Tommy. M'bale Oral wayamba madzulo awa, ndipo ine ndikuganiza akusimpina kapena chinachake, chamasuka, mu mwendo wake; ndipo mwamsanga msonkhanowu ukatha, ine ndikupita kuti ndikamupempherere iye. Ndipo tsopano kwa antchito onse a M'bale Roberts ndi antchito a M'bale Tommy, ndi kwa mipingo ndi onse: Mulungu akhale ndi inu, ndilo pemphero langa. Inu mu—inu nthawizonse muzikhala muli mu mtima mwanga, chifukwa cha nthawi iyi. Ndipo Tulsa ataima motalika, motalika ntchito ya Mulungu ikhale ili mwa iye, ndilo pemphero lathu. Ndipo ife tikuyembekeza kuti tidzabwereranso nthawiyina nkudzakhala nanu.

<sup>9</sup> Ndipo ngati ife tingakhoze konse kukuchitirani chabwino inu, mwanjira iliyonse! Ine ndinkakonda kunena chonchi: usiku siumakhala wamdima kwambiri, kapena mvula siimagwa zolimba kwambiri, koma kuti ife tingachite chirichonse chomwe chiri mu mphamvu yathu kuti tiupange moyo kukhala wawofuwofu mochuluka pang'ono ndi wodalitsika kwa inu. Ngati ife tingakhoze kukhala athandizo lililonse kwa inu, mungotilola ife kuti tidziwe. Mungotiimbira ife ku Jeffersonville, Indiana, BUtler 2-1519, kapena mungondiimbira ine ku Jeffersonville. [Telefoni nambala inasinthidwa.—Mkonzi.] Ife tikhoza kukutumizirani inu nsalu yapemphero, kukupemphererani inu, chirichonse basi chimene ife tingakhoze kuchichita. Ife ndi antchito anu mwa Ambuye.

<sup>10</sup> Kotero ndi zokhala ngati zoipa kuti tabwera ku mapeto a msonkhano monga chonchi, pamene inu mumakhala ndi nthawi yodabwitsa chotero ija, koma nthawizina ife timayenera kuti tizipita, chonchobe.

<sup>11</sup> Podziwa ichi, kuti kungowoloka Mtsinje, tsiku lina pamene moyo udzakhala wonse utatha, ndipo ine nkudzakhala pa gome lalikulu lija, lomwe lidzakhale litayalidwa mumlengalenga umo, Phwando la Chikwati, ndipo ife tizidzayang'anizana pa gomelo kwa wina ndi mzake, ife tidzakumbukira nthawi izi ku Oakland. Mosakaika, msozi waung'ono ukhoza kumadzatsikira pa tsaya lathu, chifukwa cha chisangalalo, ndipo Mfumu, mu kukongola Kwake konse, adzatulukira, mu mwinjiro Wake woyera wokondeka, kumapukuta misonzi yonse pa maso pathu, ndi kuti, "Musalire panonso. Izo zonse zatha tsopano. Lowani mu zisangalalo za Ambuye zomwe zinakonzedwera kwa inu chikhazikitsireni maziko a dziko." Ndilo ora lomwe ine ndiri kulikhalira moyo.

<sup>12</sup> Ine ndikuyang'ana mmunsi pa azitumiki anga ogwirizana nawo apa, ndi kuwona ambiri a iwo okulirapo kuposa ine. Mwinamwake akhala ali kunjira kuno pa msewu, ali ndi gitara ndi nkhotcho, akupaza njira, akuika miyala yoponderapo ndi kuwasalaza malo okumbika, kuti utumiki uwu umene Ambuye kudapatsa ine, ukhoze kuyenda mosalala podutsa mu msewuwu.

<sup>13</sup> Abale anga ofunika, ine ndikudzimverera kuchepa, kuima pamwamba pano ndipo inu muli pansu apo. Uko nkulondola. Pakakhala ulemu uliwonse woti uperekedwe, iwo upite kwa inu. Mulole Mulungu nthawizonse molemera azikudalitsani inu. Tsiku lija pamene mphotho izidzaperekedwa, ine ndikuyembekeza kuti ndidzakhala nditaima ndiripo pamene ine ndidzakuwoneni inu mukuvekedwa korona mu Ulemerero Wake.

<sup>14</sup> Mphindi pang'ono zapitazo, ine ndinali kuyankhula kwa mtumiki kumbuyo uko. Dzina lake ndi M'bale Nathan, iye anati. Iye amagwira ntchito pakati pa Ayuda. Ndipo iye anati, "M'bale Branham, usiku woyamba, pamene inu munalikuno . . ." Iye ndi mkazi wake. Iye anali akudwala. Ndipo anati, "Inu munaitana, mu msonkhano, ndipo munandiuza ine yemwe ine ndinali, ndi za mkazi wanga ndi kudwala kwake." Anati, "Iye wakhala akupeza bwino, chiyambireni pamenepo, akumangochita bwino." Ndipo pali makalata abwino ochuluka kwambiri ndi maumboni!

<sup>15</sup> Tsopano, mwinamwake inu simunalandire mpango wanu mkati muno. Ngati ife tingakhoze kukuthandizani inu, mwa njira iliyonse, kukutumizirani inu kansalu kakang'ono, tsopano, pazikhala ndondomeko yang'ono. Ife tiri ndi mndandanda wa pemphero umene ulipo kuzungulira mdziko. Anthu amauka, pa ma ora onse mu usiku, ndipo amasunga mndandanda wa pemphero uwu. Nthawizonse pa Muyezezo wa nthawi ya

Kummawa, ife timapemphera naini koloko mmawa, pa thwelofu koloko, ndi pa firii koloko. Awo ndi maora opereka nsembe a Chipangano chakale cha Chiyuda. Ndipo ife timapemphera choncho. Ndipo anthu kuzungulira mdziko amadzuka pa nthawi zosiyana, mu kulumikizana kwakukulu kwa pemphero, kumene ife tonse timapemphera limodzi, wina kwa mzake. Kotero ndine wotsimikiza kuti Mulungu amalimva pempherolo. Zinthu zodabwitsa zotero zimabweramo, zomwe Iye wazichita. Ndipo ife tikufuna kuti tikukeni inu pa mndandanda wathu wa pemphero, kuti muzipemphera nafe pa maora amenewo.

<sup>16</sup> Ndipo tsopano, mosakaika, koma posakhaltisa kwambiri, ine ndidzakakhala ndiri kutsidya kwa nyanja kachiwiri, Ambuye akalola.

<sup>17</sup> Ife tatolerapo ndalama pang'ono pano. Ndipo tiri pomwepa, Ambuye anandirola ine kuti ndinene izo kuti ine ndikhoze kukumbukira. Iwo atenga zopereka zachikondi ziwiri, ine ndikukhulupirira, kwa ine. Inu mukudziwa momwe ine ndimayamikirira izo. Tsopano, palibe wani tambala yomwe iti idzapite kwa ine ngati munthu. Izo zikupita ku thumba la mpingo la utumiki wa kutsidya kwa nyanja. Mukuona? Ndipo ife tichita zopambana kwambiri zomwe ife tingakhoze, kuti tiwone kuti ndalama zimenezo zikupita kwa anthu omwe sangakhoze kuumva Uthengawu, omwe sangathe kuti abwere. Ndipo ife tichita mwa kupambana kwathu kwambiri. Mulungu nthawizonse azikudalitsani inu molemera, ndilo pemphero langa lodzipereka.

<sup>18</sup> Ndipo tsopano, ngati inu mukufuna iliyonse ya nsalu zapemphero izi, mungolembera kwa ine. Ndi basi Positi Ofesi Bokosi 325, kapena kungoti Jeffersonville, Indiana, iyo idzabwera kwa ine. Ndipo ngati inu mukufuna kumayiika iyo mu Baibulo lanu, muziyiika iyo pa Machitidwe 19. Ndipo anthu ochuluka kwambiri andiuzapo ine.

<sup>19</sup> Dona wina anati, ine ndikukhulupira, mwana wake anali atagundidwa ndi galimoto, ndipo iye anali akuwukha pafupi kufa, pomwe anavulazidwa ndi galasi, ndipo kotero iye anathamanga mofulumira kwenikweni ndipo anakatenga kariboni aka. Iye anali mu... ankakhala mu dzikolo. Ndipo anadzaika kariboni kakang'onoko pa mnyamatayo, ndipo magazi anasiya pomwepo. Ndi zinthu zambiri zonga izo.

<sup>20</sup> Mkazi ku Germany, anapuwala. Apo amakuuzani inu zoti muzichita; muzisonkhana ndi oyandikana nawo anu Achikhristu, pamene nsalu izi ziziikidwa pa inu, cha pa mtima wanu. Ndipo iye anati, zonse zitatha kuchitidwa mwa njira yomwe izo zinaliri basi... Iye anali wopuwala kwa zaka zingapo. Ndipo anati, pamene iye anakwaniritsa zimenezo, iye anati, "Satana, tsopano iwe ulibenso malo ena a china chirichonse.

Choka pa ine.” Anadzukapo pa mpandowo ndipo anayenda nkumachokapo.

<sup>21</sup> Izo ndi zophweka chomwecho basi. Mwaona? Kotero ngati inu mungafunepo imodzi, ndi yosachita kugula, yopanda mtengo. Mungotumiza, ndipo ife tidzaitumiza iyo molunjika kwa inu, mu kalata. Tsopano, inu mudzalandira—pepala lofotokoza za momwe mungachitire izo. Koma, kumbukirani, ine ndapempherera, mwiniwanga, mwandekha, p—pa zovala zomwe ziti zidzatumizidwe kwa inu. Ngati mwana wanga akanakhala akudwala, mkazi wanga, kapena bambo anga ndi amayi, ndipo ine ndikukhala kuti ndiri nacho chidaliro mu pemphero la munthu winawake, ine sindikanafuna kuti ilo likhale pemphero la mlembi. Ine ndikanafuna kuti iwo apempherere pa izo. “Ndipo uzichita kwa ena momwe iwe ukanafunira kuti ena azichitira kwa iwe,” muyezo wagolide. Kotero, ife, ife ndithudi tidzakhala okondwa kudzakuthandizani inu mwa njira iliyonse yomwe ife tingathe. Mulungu azikudalitsani inu nthawizonse tsopano.

<sup>22</sup> Ndipo chirichonse chimene chachitidwa chachitidwa mokoma kwambiri ndi mwachikondi, ndipo ife tikungoyamikira izo mochuluka kwambiri.

<sup>23</sup> Tsopano, pamene ine ndiri kutsidya kwa nyanja, nthawizonse zimakhala zovuta. Chifukwa, mfiti zazimuna ndi zazikazi, izo sizimachita mantha kuti zikuyese iwe. Kuno posachedwapa, mu malo ena, uko kunali pafupi mfiti fifitini ku mbali iliyonse, zikuponyera matemberero pamenepo, ndipo izo zinati zikhoza kuitanitsa nkuntho ndipo iwo ukhoza kundikupiza ine ndichokepo. Ndipo, khulupirirani izo kapena ayi, nkunthowo unabwera. Pafupi anthu sate sauzande, ndi malowo akugwedezeke mwamphamvu basi momwe iwo akanathera.

<sup>24</sup> M’bale Arganbright, wa Christian Business Men, inu abale mukumudziwa iye. Iye anali atakhala kumbuyo kwa ine. Iye anati, “M’bale Branham.”

<sup>25</sup> Ine ndinati, “Ingokhala bata. Mzimu Woyera unandituma ine kuno.” Ndicho chifukwa ine sindimapita ku malo kupatula ngati Iye atandituma ine poyamba, ndiye ine ndimadziwa ine ndikhoza kubwera mu Dzina la Ambuye. Mwaona? Ine ndinati, “Iye anandituma ine kuno.”

<sup>26</sup> Iwo anali atamanga malo aakulu kwambiri, basi komwe iwo amakhala ngati ndi ma thuu-bai-foro, ndi chirona chitaikidwa pamwamba pake. Ndipo malo amenewo anali akungonyamuka mmwamba ndi pansu. Kumene mu... pafupi thuu koloko madzulo. Kowala basi monga iko kukanakhalira kuli, ndipo nkuntho uwo unabwerapo mu maminiti sate. Ndipo ine ndinangoima. Ine ndinati, “Inu simukusowa kuti mutanthauzire izi.” Ndikumverera mphamvu yoipa iyo ikuchokera ku mbali iliyonse. Ndipo iwo atakhala pamenepo, anali akutembenuza

manja awo ndi nthenga zodulidwa, ndi sizesi. Inu mukudziwa momwe iwo amachitira.

<sup>27</sup> Ine ndinati, “Ambuye Mulungu, Mlengi wa miyamba ndi dziko lapansi, Inu munali Yemwe munanditumiza ine kuno. Inu muli ndi udindo pa utumiki umene ine ndikukutengerani Inu. Ine ndikuudzudzula nkuntho umenewo, mu Dzina la Ambuye Yesu.”

<sup>28</sup> Ndipo unangokungunukira mmbuyo momwe. Mabingu anabingula mokutha, ndipo dzuwa linali kuwala, mochepera maminiti awiri, pansu pomwe. Ndipo zikwi anathamangira ku guwa, ndi oganiza mwa chikominisi ndi chirichonse. Momwe. . .

<sup>29</sup> Ine sindingakhoze kuima pano ndi kumakuuzani inu maumboni, chifukwa ndi mu msonkhano wanga womwe. Izo zikanakhala bwino kuti ena azichita izo. Koma, laibulare, ine ndinganene kuti pakhoza kukhala insaikulopidia, pakhoza kukhala mabuku ochuluka kwambiri atalembedwa, zomwe ine ndawaona Ambuye Yesu akuzichita mu utumiki wanga womwe waung'onowu. Kodi inu mukuganiza kuti mukanakhala chiani mwa amuna awo monga M'bale Tommy Osborn, M'bale Oral Roberts? Ndi zazikulu. Ambuye wathu ndi wamkulu. Ndithudi ali.

<sup>30</sup> Tsopano ine ndikufuna kuti ndiwerenge Lemba lina, madzulo ano. Ndipo ine ndiri nawo malo angapo ndawalemba apa, ngati ine nditi ndifike kwa iwo. Ndiyeno ife tiri. . . Ine ndikukhulupira mwana wanga wandiuzwa ine kuti iye wagawa makadi ena apemphero, ndipo ife tiwapempherera odwala.

<sup>31</sup> Ngati ine sindidzaika maso pa aliynese wa inu nonse kachiwiri, ngati ine sindidzakuwonani konse inu mu moyo uno; pamene ine ndidzakomana nanu inu pa Chipata icho, ife tisanakalowe umo kuti tikaima pamaso pa Khristu, masomphenya ochokera kwa Mulungu ndi owona ndi enieni. Mngelo wa Ambuye, ndilo Lawi Lamoto ndi Kuwala, chotero ndithandizeni ine, Mulungu Wamphamvuzonse, Wondiweruza wanga, Izo ziripo. Izo nzoona. Eya. Kotero kuti inu mudziwe kuti I—izo nzoona. Mulungu ndi woona. Iye sangakhoze kukhala wabodza nkukhala Mulungu. Iye ali wo- . . . Iye sangakhoze kukhala wabodza, chifukwa Iye ayenera kukhala weniweni. Ngati chirichonse chiri chabodza, ndi Satana. Koma Kuwala uko, ine ndakuwonapo Iko, ndayang'anapo pa Iko. Ndipo kwa ine. . . Chonde mundikhululukire ine ngati ine ndikuchita mosinjirira, koma, kwa ine, ndi Lawi la Moto lomwe lija lomwe linkawatsatira ana a Israeli.

<sup>32</sup> Chifukwa, Ilo linkakhala mwa Mwamuna wotchedwa Yesu, yemwe anali Mwana wa Mulungu, ndipo moyo umene Iye ankakhala ukuwonetseredwa kachiwiri lero mwa chinthu chomwecho. Iye anati, “Ine ndinachokera kwa Mulungu. Ine ndikupita kwa Mulungu.” Ife tonse tikudziwa zimenezo. “Ine ndinachokera kwa Mulungu, ndipo Ine ndikupita kwa

Mulungu.” Iye anati, “INE NDINEYO.” Ilo linali Lawi la Moto. Uyo anali Mngelo yemwe anali mu thengo. Iye anapangidwa thupi ndipo anadzakhala pakati pathu; anabwerera kachiwiri. Ndipo Ilo liri mu mawonekedwe omwewo lero. Kodi inu mumazidziwa zimenezo?

<sup>33</sup> Chabwino, Inu mukuti, “Yesu anali...” Chabwino, ine ndiri—ine ndikuyankhula za Mulungu, yemwe anali mwa Yesu.

<sup>34</sup> Pamene Paulo anali pa ulendo wake waku Damasiko, Kuwala kunamukanthira iye pansi, Lawi la Moto. Palibe wina wa iwo analiwona Ilo, koma Paulo analiwona Ilo. Ilo linali mochuluka kwambiri mpaka Ilo linamupangitsa iye khungu. Ndipo iye anati, “Ndinu Yani, Ambuye?”

<sup>35</sup> Iye anati, “Ine ndine Yesu.” Iye anali atabwereranso kwa Mulungu, komwe Iye anachokera.

<sup>36</sup> Kwa ine, Ndi Iyeyo kachiwiri lero, akutsirizitsa ntchito Zake mwa ife, Mpingo, mu masiku otsiriza.

<sup>37</sup> Tiyeni titembenzire ku Deuteronome 32:11, kwa maziko pang’ono a nkhaniyi. Ndipo ife tiyesera kuti tikhale ndi mzere wa pemphero, ndipo tikhale titatuluka mkati mwa ora, ngati zingatheke. [Mlongo akupereka ulosi—Mkonzi.]

<sup>38</sup> O Atate Mulungu, momwe modzichepetsa mu mtima mwanga ine ndikuzilandirira izo. Atsogolereni mapazi anga, gwirani dzanja langa, Ambuye. Ndisadzakhale konse mwala wopunthwitsa kwa aliyense, koma mulole ine ndikhale mwala woponderapo kwa woyenda paulendowu. Perekani izi, Ambuye. Mulole ine ndisadzachite kalikonse mu moyo wanga komwe kati kadzaike mthunzi pa Dzina Lanu, kapena pa cholinga Chanu. Ndipo ine ndizichita zonse zomwe ine ndingathe kuti ndizikutumikirani Inu. Ine ndikukuthokozani Inu chifukwa cha izi, mu Dzina la Mwana Wanu, Yesu Khristu, Ambuye wanga. Amen.

<sup>39</sup> Momwe izo zikuuchepetsera mtima wanga! Deuteronome 32:11, “Monga m...” [Mlongo apereka ulosi—Mkonzi.] Amen. [Mlongo wina apereka ulosi.] Amen. Lidalitsike Dzina la Ambuye. [Mlongo wina apereka ulosi.] Momwe ife tikuwathokozera Ambuye, kuti tiri nawo Mzimu Wake ukugwira ntchito pakati pathu, pakati pa ife!

*Momwe mphungu ikasulira chisa chake, nikapakapa pa ana ake, itambasulira mapiko ake apo, nkuwatenga iwo, nkuwanyamula iwo pa mapiko ake:*

<sup>40</sup> Uko si mochuluka kwambiri kuweringa kwa Lemba, koma Awo ndi Mawu a Ambuye. Ndi zokwanira apo kuti, mwinamwake, Mulungu atipatsa ife nkhani kuchokera apa, mu maminiti otsatira twente kapena sate, zomwe ziti ziwapangitse anthu kuwuka ndi kumaganizira za Ambuye Yesu.

41 Inu mukudziwa, nthawiyina, ine ndinawerenga nkhani, zaka zingapo zapitazo, mu *Moyo Wa Abraham Lincoln*. Kunali mwamuna mu ndende, ndipo iye anali pansi pa chiweruzo cha feduro, ndipo iye anali woti adzawomberedwa. Ndipo bwenzi wake wabwino anapita kwa Purezidenti, Abraham Lincoln, bambo Wachikhristu wodabwitsa. Ndipo iye anati, “Bambo Lincoln, ine ndikudziwa kuti inu ndi munthu wabwino, kuti ndinu Mkhristu. Ndipo pansi pa chiweruzo cha feduro ichi, poti bambo uyu waphwanya lamulo la zotsatira za ankhondo. Iye ndi mzanga. Iye samatanthauza kuti achite zimenezo. Iye walakwa pochita izo. Iye samatanthauza kuti achite izo. Kodi inu chonde. . . Ndinu munthu yekhayo yemwe angakhoze kupulumutsa moyo wake. Kodi simuupulumutsa moyo wake?” Ndipo ulemu wa Bambo Lincoln ananyamula cholemba chake ndipo analemba pa chidutswa cha pepala, chifukwa iye sanali pa desiki yake pa nthawi imeneyo, kuti apange chidindo chovomerezeka. Ndipo kotero iye analemba pamenepo, “Ine ndikumukhululukira munthu uyu,” ndipo analembapo dzina lake, “Abraham Lincoln.”

42 Mzake wofunika wa munthu uyu anathamanga molimba momwe iye akanakhoza kuchitira, waku ndende, ndipo anati, “O, bwenzi wanga, ndiwe mfulu. Ndiwe mfulu. Dzina la Purezidenti ndi ili pa chidutswa cha pepala ichi. Iwe wakhululukidwa.”

43 Ndipo bamboyo anati, “Usandipusitse ine, chifukwa ine ndakonzekera tsopano kuti ndife, chifukwa ine ndaweruzidwa kuti ndiphedwe. Ndipo apa iwe ukubwera kudzanditonza ine ndi chidutswa cha pepala. Ngati chidutswa cha pepala icho chikanakhala chikhululukiro cha Abraham Lincoln, icho chikanakhala chonse chitakongoletsedwa ndi zisindikizo ndi zina zotero.”

44 Iye anati, “Bwana, ili ndi dzina la Purezidenti. Iwe wakhululukidwa.” Ndipo bamboyo anatembenezira nsana wake kwa icho ndipo sanafune kumvetsera kwa izo.

45 Mmawa wotsatira, masana kukuwala, bamboyo anawomberedwa patsogolo pa gulu lowombera. Tsopano, apa pali chikhululukiro chochokera kwa Purezidenti, chomwe chikuti, “Musamuphe munthuyo,” chinasainidwa tsiku lina. Tsiku lotsatira, munthuyo anawombeledwa.

46 Ndiye mulanduwo unakaweruzidwa mu mabwalo a feduro. Ndipo pamene bwalo, Bwalo lamilandu la Federal ya United States of America linazenga mulanduwo, ndipo lingaliro la bwalo la mulanduwo linali ili. “Chikhululukiro sichimakhala chikhululukiro kupatula icho chikakhala chitalandiridwa ngati chikhululukiro.”

47 Ndipo umu ndi momwe Mawu a Mulungu aliri. Iwo ndi machiritso kwa inu, ngati inu muwalandira Iwo ngati



machiritso. Iwo ndi chikhululukiro kwa inu, ngati inu muwalandira Iwo ngati chikhululukiro. Dalitsa lililonse mkati *Umu* ndi lanu ngati inu mulilandira Ilo mwa njira yomwe Mulungu analemba Ilo.

*Momwe mphungu ikasulira...chisa chake, nikapakapa pa ana ake, . . .niwatengera iwo pa mapiko ake, ndi kuwanyamula iwo.*

<sup>48</sup> Ndi nthawi zingati zomwe ine ndaganiza momwe Mulungu amafanizirira cholowa Chake, kwa mphungu! Ndipo ine ndimapeza, mu Baibulo, kuti Mulungu amadzitcha Yekha mphungu. Iye ndi Yehova mphungu. Ndipo kodi Iye akanachita motani izo?

<sup>49</sup> Kotero, ndine wazachirengedwe. Kotero ine...Baibulo langa loyamba linali chirengedwe. Ngati inu mutati mungoyang'ana momwe chirengedwe chimagwirira ntchito, inu mukhoza kumupeza Mulungu. Kulikonse kumene inu mungayang'ane, inu mumuwona Mulungu, ngati inu mutamatengera Mulungu mu mtima ndi kumapenya izo. Tsopano, pamene iwo amayankhula za kulowamuthupilina ndi zinthu, izo ndi zopusa; izo sizingakhoze kukhala.

<sup>50</sup> Ife tikupeza kuti mbewu zimafa, zimapita mu nthaka; mbewu imavunda, iyo imakhalanso moyo. Ndi chiukitsiro. Ndipo Chikhristu chonse chakhazikika pa chiukitsiro. Ndipo ife tikhoza kuwona kuti izo nzoona; imfa, kukwiriridwa, chiukitsiro; zirimwe, zisanu. Chirengedwe chonse chimalumikizana momwemo.

<sup>51</sup> Baibulo langa loyamba, linali kumawona momwe mitengo iyo imafera, momwe mphukira zimaphukira pamwamba kachiwiri; momwe mphepo imakupizira pa izo, izo zimabwerera kachiwiri; momwe duwa laling'ono limafera, kukhala moyo kachiwiri. Ndi zinthu zonse zosiyana izo, izo zinandipangitsa ine kudziwa kuti ilipo mphamvu ya chiukitsiro kwinakwake.

<sup>52</sup> Tsopano, mtengo uli ndi moyo wopitirira. Ife tiri ndi Moyo wachisavundi. Mtengo udzafika ku mathero ake otsiriza. Ife sitingakhoze konse; ife tiri ndi Moyo wachisavundi.

<sup>53</sup> Tsopano, ine ndinayamba kuziphunzira mphungu pamene ine ndinawerenga izi. Nanga mphungu yatani? Ine ndinadzapeza kuti mphungu ndi mbalame yosamvetsetseka kwambiri. Iyo imakhoza kuuluka pamwamba kuposa mbalame ina iliyonse yomwe ilipo. Iyo ndi mbalame yomangidwa mwapadera. Iyo imamanga chisa chake mu miyala, patali pomwe pamwamba. Iyo ndi mbalame yosamvetsetseka. Ndipo chinthu china, nthenga zake ndi zolimba kwambiri iwe sungakhoze, nkomwe, iwe sungakhoze kuzizula izo ndi pulayala. Iyo ndi mbalame, yayikulu yokhuthala, imodzi ya zokulitsitsa zomwe ziripo. Ndipo iyo ndi mbalame yosamvetsetseka kwambiri. Koma iyo

inamangidwa mwapadera chifukwa iyo ili ndi ntchito yapadera yoti izichita.

<sup>54</sup> Mawu akuti *mphungu* amatanthauza “wokhadzula ndi mulomo.” Ndipo iye amadyetsa ndi mulomo. Chinthu chokongola kwambiri cha Mawu a Mulungu, amadyetsedwa kuchokera mu kamwa kwa kamwa, Mulungu akuwadyetsa ana Ake.

<sup>55</sup> Ndiyeno iye amamanga chisa chake pamwamba, ndipo iye amachita zimenezo ndi cholinga, ndi chirichonse. Tsopano, ngati...Mphungu inali ndi mapiko amphamvu kwambiri. Amenewo ndi a chiwombolo.

<sup>56</sup> Ndipo chinthu china chimene mphungu imachita, ndi chachirendo, iyo imadzibwezera unyamata wake. Mphungu, pakapita nthawi yaitali kwambiri, imangodzisintha ndi kubwereranso kukhala mphungu yaing’ono kachiwiri, kudzibweretsa yokha mmbuyo momwe. Iyo imadzibwezera unyamata wake.

<sup>57</sup> Icho ndi choimira china cha Mpingo, wa anthu a Mulungu. Ife timafika yense pansi ndi kukhala ngati osakondweretsedwa, ndiye, zonse mwakamodzi, Mzimu Woyera umadza ndi kudzatipanga ife atsopano kachiwiri. Mulungu, kupanganso chotichitikira ndi unyamata wa Mpingo Wake, kuwapatsa iwo chowachitikira chatsopano. Icho ndi choimira cha mphungu.

<sup>58</sup> Zaka zina zapitazo, ine ndinkachita zokwera kwambiri, kodyetsera ziweto, ndipo ife tinali uko ku Troublesome River mu Colorado. A Hereford Association amadyetsera ku msipu wa Arapaho uwo kumeneko, ndi zina zotero, ndi kuntunda kuzungulira mapiriwo. Ndipo ife tinkazitengera ng’ombe kuntunda uko. Ndiyeno, pa kugwa masamba pa chaka, ife timakazisaka izo uko kachiwiri, kukaziyika izo ku National Forest. Ndiye ife timaweta msipu wathu pansi kumusiko, kuti tizidzazidyetsa, kupyola mchisanu.

<sup>59</sup> Ndipo ine ndikapita uko chaka chirichonse, kuti ndikasake. Ine ndikumachita, panobe. Ndipo bwenzi wanga, ife timakhoza kubwerera uko, anthu onse ochokera ku mizinda atafikako uko kale ndipo atawombera konseko, ana a agwape, ndi ana a sekhwe, ndi ng’ombe zazing’ono, ndi nkhuzi zovutika zokalamba za mphalapala zomwe ziri pansi mmusimo. Moti, ife nthawizonse tinkapita ulendo wonse, pamwamba, kumene iwe sungakhoze kufikapo, ndi kukazika msasa kumeneko. Iye akatenga mbali yakummawa, kummawa kapena kumadzulo, imodzi, ndipo ine ndimatenga inayo. Ife timakhala ndi masiku angapo ife tisanakomane wina ndi mzake.

<sup>60</sup> Ine sindidzaiwala konse, chaka china, iko sikunachite chisanu, umo munali mu Okotobala pamene nyengoyo imabweramo.

61 Ndipo ngati kuchita chisanu mmwamba mu mapirimo... Moti, mwinamwake, mu Okotobala, uko kumakhala m—madzulo okongola kwenikweni, mwinamwake mu ora lina kumakhala kukuchita chisanu. Ndiye imavumba nkuchichotsapo, ndiyeno dzuwa limatuluka, kumangosintha nyengo. Komano, pamene chisanu chibwera, icho chimathamangitsa agwape ndi mbawala, zazikulu izo zomwe zimakhala pamwamba, kutali ndi phokoso la chitukuko, icho chimazithamangitsira izo kupita ku zigwa. Ndi pomwe inu kawirikawiri mumatengera chikho.

62 Chaka ichi, zisanu zinali zisanabwere apobe, ndipo ine ndinali patali pamwamba apo. Ndipo ine ndinali nditamusiya kavalo wanga mmbuyo mailosi angapo, ndipo ndinali nditamumangirira iye, mokuti iye akhale ndi malo ochuluka; msipu wina, chotero kuti iye azikhoza kumadya. Ndipo ine ndinali nditapita ulendo wonse cha ku malire a mitengo, kumtunda uko, ndikuyang'ana.

63 Madzulo amenewo uko kunadza nkuntho ukusesa kudutsa mmapiri, n—ndi kubangula kwa bingu, ndi kung'anima kwa mphenzi. Ndipo ine ndinapita paseri pa mtengo. Ndipo ine ndinaima mmbuyo kuseri kwa mtengo mpaka nkuntho utatha, ndinatsikiranso mu mitengo. Panali wogwetsedwera-pansi apo. Ndipo ine ndinali nditaima kuseri kwa mitengo, ndikuyembekezera mpaka nkuntho udutse; nditaima apo, ndikuganiza. Ndipo ine ndinali ndi mfuti yanga itangotsamira p—pa mtengo. Ndiyeno pamene n—nkuntho unatha... Ine ndinali ndikuganiza za Mulungu, momwe Iye analiri wodabwitsa.

64 Ndipo pamene nkuntho unali kuchitika, mphepo yozizira inayambikamo, ndipo iyo inaumitsa madzi ochuluka kobiriwira nthawizonseko, monga tizisanu tikulendewera. Ndiye pamene dzuwa linatulukira, mmbuyo momwe kutali, kumadzulo, ine ndimakhoza kuliwona dzuwa likungosuzumira kudutsa mming'aru ya phiri, ndi kumawoneka ngati diso la Mulungu.

65 Inu mukudziwa, Mulungu aliponseponse. Inu mukhoza kumuwona Iye basi, kulikonse, ngati inu mutati muzimufunafuna Iye. Iye ali pamenepo. Inu mumayenera kuti mumuwone Iye. Iye akhala ali pano. Iye ali pano pakali pano. Ngati inu mutati muyang'ane pozungulira, inu mumuwona Iye.

66 Ndiyeno pamene ine ndinali nditaima apo, ine ndinayang'ana pa iko—kulowa kwa dzuwa uko. Ndipo ine ndinakweza mmwamba manja anga, ndipo ine ndinati, “O Yehova Mulungu wamkulu, maso Anu akuyang'ana uku ndi uko, kudutsa padziko lapansi.”

67 Basi pomwepo ine ndinamva phokoso lochokera k—kwa mphalapala yamphongo. Iye anamwazikira kutali ndi gulu, mu nkuntho, ndipo iye anali kupanga kulira kwenikweni kwakuthwa kuja kwa phokoso monga choncho. Ine ndinamva

gululo likumuyankha iye, cha kuno mu malo ena. Ndipo kutali uko ku mbali ya phiri, nkhandwe yokalamba yotuwa inayamba kuwuwa; imzake inayankha, kumusi pansi. Ine ndinayang'ana pozungulira, kudutsa chigwacho, kuchokera ku phiri limodzi, kudutsa pogawaniza, apo panali utawaleza. Chabwino, basi kulikonse kumene ine ndinali kuyang'ana, uko kunali Mulungu.

<sup>68</sup> Amayi anga ndi theka Mmwenye. Iwo anachokera ku malo otetzedwa, ndi Mmwenye wachi Cherokee. Ndipo amayi awo ankalandira zachipepeso. Kutembenuka kwanga sikunazichotse konse izo mwa ine. Pali chinachake chokhudza mnkhalango ndi kutali ndi makomo zomwe ine ndimazikonda.

<sup>69</sup> Pamene ine ndinaimva nkhandwe yokalamba iyo ikuwuwa, ndipo imzake ikuiyankha iyo, misonzi inayamba kugwera pa masaya anga. Ine ndinamumva gwape wamphongo wokalamba uyo akufuula pamwamba apo, pofuna gulu lake. Ilo linayankha. Ine ndinayang'ana pa utawaleza. Ine ndinati, “Eya. Ndi uyo Mulungu, kachiwiri.” Iye ali Alfa ndi Omega. Iye ali mitunduyo, pangano, mu utawaleza. Mulungu amakhala paliponse, ngati inu mutati muzingomufunafuna Iye pamenepe.

<sup>70</sup> Ine ndinakhala wosangalala kwambiri! Ine ndinangokweza mmwamba manja anga, ndi misonzi ikutsikira pansi pa masaya anga. Ine ndinathamanga chozungulira, ndi kuzungulira ndi kuzungulira mtengo umenewo. Ine ndinali nayo basi nthawi yopambana, ndipo panalibe wina mu mailosi sate a ine; ndimangolumphira mmwamba ndi pansi, ndi kumafuula mokweza mawu anga. Moona, ngati pakanati pakhale winawake akundiyang'ana ine, iwo akanaganiza ndi winawake wochokera ku malo azamisamala anali kumeneko. Koma ine sindinali kusamala. Ine ndinali ndiri ndi nthawi yabwino. Ine ndinali ndikupembedza Ambuye, Mulungu wanga. Sizinapange kusiyana kulikonse kwa ine chomwe wina aliyense akanaganiza. Ndipo ine ndinalikungokhala ndi nthawi yabwino, kumangozungulira, ndi kuzungulira zungulira mtengo umenewo. Ine ndimakhoza kuima, kumvetsera kwa nkhandwe iyo, ndi kumvetsera izo. Ndi kufuula kachiwiri, kuzungulira, zungulira mtengowo ine ndimakhoza kuzichita kachiwiri.

<sup>71</sup> Ndipo i—ine ndinapangitsa chinachake kutengeka. Ndipo apo panali gologolo wamng'ono wa mu paini. Ine sindikudziwa ngati inu mumadziwa chomwe iwo ali kuno mu Oklahoma, kapena ayi. Kanthu kakang'ono basi kaphokoso pafupi kotalika *choncho*. Iye ndi msirikali wa chikhotho-cha buluu wa mnkhalango. Iye basi. . . Iye amapanga phokoso lochuluka kwambiri, ndipo iye si kanthu. Ndipo iye analumphira pamwamba pa chitsa, ndipo iye anayamba chata, chata, chata, basi molimbika momwe iye akanathera. Ndipo ine ndinaganiza, “Palibe chifukwa choti iwe utengeke. Ine ndikuwapembedza Ambuye. Iwe sukuzikonda zimenezo? Taona izi.” Ndipo ndinazungulira, ndi kuzungulira, ndi ku zungulira,

ndipo kuzungulira kachiwiri, ine ndinkachita, mwamphamvu basi momwe ine ndikanathera. Ndipo ine ndinati, “Kodi sizodabwitsa zimenezo? Mlengi wako; Mulungu wanga!” Tiye tichite izo kachiwiri, kuzungulira, ndi ku zungulira, ndipo kuzungulira monga choncho.

<sup>72</sup> Ndipo ine ndinazindikira kanthu kakang’onoko kakupendeketsera mutu wake waung’onowo chammbali, ndi kumayang’ana pansu ku wogwetsedwera-pansu uwo. Izo sizimawoneka ngati ndine ndamupangitsa iye kutengeka. Panali chinachakenso chimamupangitsa iye kutengeka. Chabwino, ine ndinaganiza, “Usaganize kuti ine ndikuchita mwachilendo. Chifukwa, ine sindikuchita mwachilendo, kwa mwiniwanga. Ndipo ine ndikudziwa kuti Iye akundidalitsa ine, kotero iwe ukhoza kumangochita limodzi nane.”

<sup>73</sup> Ndipo kotero ine ndinapezeka nditayang’ana. Ndipo nkuntho unali utaikakamizira mphungu yaikulu pansu. Ndipo iyo inamakamizira iye pansu umo. Iyo inali itatsikira pansu, mwinamwake imadya. Iyo siikanakhoza kupeza mphamvu zake, pamwamba pake, kuti ikafike pamwamba pa nkuntho, kotero iwo unaikakamizira iyo pansu mu thengo. Ndipo apo iyo inali, itatsikira pansu pa ili—tchire ili kuno.

<sup>74</sup> Ndipo ndi chimene chinali kumupangitsa gologolo wamng’onoyo kutengeka. Ndipo iye anali akumuyang’ana uyo mwatcheru kwenikweni, akuchita choncho, kuti chata, chata, chata, chata, ngati kuti akanakhoza kuikhadzula mphungu iyo mzidutswa. Chabwino, iye sanali wamkulu mokwanira kuti angakhadzule kanthu kena mzidutswa. Kotero iye anali ataima pa chitsa icho, mchira wake waung’onowo utapindikira mmwamba monga *choncho*, kumangoti chata, chata; chata, chata, chata, chata. Ine ndinaganiza, “Chabwino, usati utengeke. Iye sakupweteka iwe.”

<sup>75</sup> Ndipo mphungu yaikulu iyo inalumphira pa nthambi, monga *choncho*. Ine ndinaganiza, “O Mulungu, ndi Inu uko, mu kuitana kwa nkhandwe uko. Ndi Inu apo, cha kuno, mu kuitana kwa mthengo. Ndi Inu uko, mu kulowa kwa dzuwa. Ndi Inu uko, mu utawaleza. Nchifukwa chiani inu munayiika mphungu iyo patsogolo pa ine? Chiani, kodi mphungu iyo ikuchita chiani pamene? Ine sindikukhoza kukuwonani Inu mu mphungu imeneyo.”

<sup>76</sup> Ine ndinaiyang’ana mphungu imeneyo. Ine ndinati... Ndinayang’ana pa iyo, maso ake owoneka-motuwawo. Iye sanali kumusamala gologolo wa mpaini uyo, mochulukwa kwambiri. Iye anali kundipenyetsetsa ine. Ine ndimakhoza kuwaona maso akulu awo akundiyang’ana ine. Ndipo ine ndinaganiza, “Chabwino, eya, ine ndikukhoza kumuwona Mulungu mwa mphungu iyo, chifukwa chakuti iyo sikuchita mantha. Pali

chinachake pa iye, kuti iye sakuchita mantha.” Ine ndinati, “Ine ndiyesera, ndi kuwona ngati iye akuchita mantha.”

<sup>77</sup> Ine ndinati, “Ndinati, mwanawe, iwe ukudziwa ine ndikhoza kukuwombera iwe?” Ine ndinati, “Iyi ndi mfuti yanga. Ine ndikhoza kukuwombera iwe.”

<sup>78</sup> Iye anangoyang’ana apo pa ine, monga *choncho*. Ine ndinapitirira kuzindikira kuti iye amamverera mapiko ake. Ine ndinati, “Ine ndawona tsopano. Ndi chifukwa chake. Iwe sukuchita mantha, chifukwa chakuti Mulungu anakupatsa iwe mapiko awiri. Ndipo iwe ukudziwa, bwino bwino, iwe ukhoza kukhala uli mu mtengo umo apo ine ndisananyamulire konse mfuti iyo mu dzanja langa.” Ine ndinaganiza, “Ngati iwe ungakhoze kudalira mapiko ako opatsidwa ndi Mulungu, kuti uthawe ku choopsya, ndi mochuluka bwanji momwe Mpingo uyenera, uli ndi Mzimu wopatsidwa ndi Mulungu, wa Mzimu Woyera pakati pathu, kuti uzithawa ku zinthu, kuchokako kwa izo, monga *choncho*.” Ine ndinkamupenya iye, momwe iye amawamvererera mapiko awo. Bola ngati . . .

<sup>79</sup> Winawake anati kwa ine nthawi ina, “M’bale Branham, kodi inu simumachita mantha kuti mungalakwitse?” Ayi, bwana, osati pamene ine ndikumverera Chinachake icho pondizungulira ine. Izo zonse ziri bwino. Ziri bwino. Bola ngati Iye alipo, ndi Iyeyo azichita izo.

<sup>80</sup> Ndipo ine ndinkaipenya mphunguyo kwa utali wa nthawi. Ndipo iyo inawona kuti ine ndimaikonda iyo mochuluka kwambiri, ine sindikanati ndiivulaze iyo. Ndipo kotero iyo siimachita mantha nane, koma iyo inangonyansidwa ndi chata, chata; chata, chata, chata uyo. Ndipo iyo inatopa nazo, kotero iyo inangopanga kudumpha kumodzi kwakukulu, inakupiza mapiko ake pafupi kawiri. Ndiyeno ine ndinawona chifukwa chomwe iye anandisokonezera ine ndikufuula. Mphungu yaikulu iyo siinakupize konse mapiko ake kenanso. Iyo inangowoneka kuti imadziwa momwe ingawaikire mapiko ake. Ndipo nthawi iliyonse mphepo ikabweramo, iyo imangokwera mmwamba. Ndipo mphepo ikabwera umo, iyo imakwera mmwamba. Ndipo ine ndinaima apo ndipo ndinkaiyang’ana iyo mpaka iyo inangokhala kadontho kakang’ono kwambiri. Ndipo ine ndinati, “O Mulungu, ndi zomwe ziri.” Iye anali atatopa ndi chata, chata, chata uja.

<sup>81</sup> Si ndizo, “Kuthawa kuchokera ku tchalitchi kupita ku tchalitchi. Kujowina *uwu* ndi kujowina *uwo*.” Ndi kungodziwa momwe ungawaikire mapiko ako mu mphamvu ya Mzimu Wake Woyera. Pamene Iye abwera nkukwera umo, muzingokwera mopitirira, kumakwera, kupitirira pitirira pitirira. Pitani kutali ndi chata, chata uyu, “Masiku a zozizwitsa anapita. Palibe chinthu chotero monga Mzimu Woyera. Ndinu olakwa nonse, mu *Izi*. Palibe chinthu chotero monga machiritso

Auzimu.” Muzingokwera, pamwambabe pa izo. Muzingoulola Mzimu Woyera uzikwera umu, ndi kukwera kupitabe kutali. Kumangopitirira, patali ndi mmwamba, komwe mtunda siwoti ungamvedwenso. Mai!

<sup>82</sup> Mulungu anaipanga mphungu. Tsopano, ngati iyo ikanati isakhale. . . Ngati kantema atayesera kuti ayitsatire mphungu, iye anganyenyekere mu mlengalenga. Khwangwala atayesera kuti aitsatire iyo, nthenga zingathothoke pa iye. Iye ndi mbalame yopangidwa-mwapadera.

<sup>83</sup> Mulungu amayerekeza mphungu Zake monga aneneri Ake. Mneneri amakwera mmwamba kupita mmilengalenga komwe iye amakhoza kuyang’ana patali.

<sup>84</sup> Tsopano, ngati mphungu ili nawo mapiko aakulu, amphamvu omwe angakhoze kumutengera iye mmwamba umu. Ndipo, maso ake akanati asamafanane ndi mapiko ake, iye akanamakhalala wakhungu pamene afika mmwamba umu. Ndi chifukwa kantema, akayesera kuti akhale mphungu, pamene iye akwera mmwamba kwambiri, iye sangakhoze kuwona, mulimonse, kotero izo sizingamuchitire iye ubwino uliwonse kukwera mmwamba. Mwaona? Iyo ndi mbalame yopangidwa-mwapadera.

<sup>85</sup> Ndipo Mkhristu ndi munthu wopangidwa-mwapadera. Ndizo ndendende kulondola. Palibe chifukwa chomapitira ku tchalitchi, kupatula ngati iwe uli nacho Chinachake chimene chimakuuza iwe kuti zonse ziri mmenemo. Mwaona? Ndi chinachake chapadera chimene Mulungu amakuchitira iwe.

<sup>86</sup> Mphungu iyo ikhoza kupita mmwamba kwambiri mpaka inu simungakhoze kuiwona iyo, ndipo iyo ikhoza kumawona chirichonse chikuyenda pansipo, kanthu kakang’ono ng’ono; diso lake ndi lopambana kwambiri.

<sup>87</sup> Nthawi ina yapitayo, zaka zitatu kapena zinai zapitazo, msungwana wanga wamng’ono ndi ine tinali kuyenda uko kosungira nyama ku Cincinnati. Ine ndinali ndi iwo uko Loweruka lina madzulo, ndikuwasonyeza iwo zinthu zosiyana. Ndipo Sarah wamng’ono ndi ine tinkayenda apo, iye anali msungwana wamng’ono kwambiri pamenepo, basi pafupi usinkhu wa zaka zitatu. Ndipo ife tinali kuyenda apo. Ndipo apo panali mphungu yaikulu mu khola.

<sup>88</sup> Ndipo ine nthawizonse ndinkadana nazo kuwona nyama zitatchingidwa. Ine sindikudziwa, ine ndimangodana nazo kuiwona mbalame ya chingolopiyo. . . Ine sindiri kuponyera kumbali, pa apumbwa anu ndi zinthu, koma ine sindimakonda kuwona kanthu kalikonse mu khola. Ine ndikudziwa momwe zimakhalira ukakhala utatchingidwira mu chipembedzo kumene iwe ulibeko ufulu. Tsopano, i—i—ine ndimafuna ku. . . Ine ndimakonda kuti ndizikhala mfulu.

<sup>89</sup> Ndiye, zimangokhala ngati kuipatsa mbalame yanu ya chingolopiyo mavitamini onse omwe mungathe, kuti apange nthenga zabwino ndi mapiko abwino, ndiyeno nkumaisunga iyo mu khola. Ndi ubwino wanji womwe zimamchitira iye?

<sup>90</sup> Ndi ubwino wanji womwe zimawachitira kuwatumiza alaliki kutali ku maseminare ndi zina zotero, ndi kuwaphunzitsa iwo, chirichonse monga choncho, ndiyeno nkuwaika iwo mu khola, pa kunena kuti, “Masiku a zozizwitsa anapita. Palibe chinthu choterocho”? Ndi ubwino wanji zimawachitira kuwaphunzitsa iwo? A . . .

<sup>91</sup> M'bale, ine ndimakonda chinachake chomasuka, kumene iwe ungakhoze kumauluka ndi kumayeserako wekha, chipembedzo chimene chimakulola iwe kuti uzimasuka.

<sup>92</sup> Ine ndinazindikira panali mphungu yaikulu iyi. Iwo anali atangoigwira kumene iyo, nkuiyika iyo mu khola. Ine ndinaganiza awo anali mawonekedwe omvetsa chisoni kwambiri omwe ine ndinayamba ndawaonapo. Chinthu chachikulu kwambiri icho, iyo inali itagona pansi apo, pamene ine ndinkafika apo, mapiko ake aakuluwo ali otambasulidwa. Nthenga zonse zinali zitathothoka pa mutu wake, ndi cha pa khosi lake ndi kumapeto a mapiko ake. Ine ndinayang'ana pa iye.

<sup>93</sup> Iye anakwawa kudutsa mkholalo. Iye anayang'ana mmbuyo kudutsa mkholalo, monga *choncho*. Uyu akubwera apayu, ndipo iye analigunda kholalo ndi mutu wake ndi mapiko, akungokupiza. Nthenga zimakhoza kumathothoka. Iye amagwera mmbuyo. Iye amakhoza kudzukapo kachiwiri. Iye anabwerera mmbuyo njira *iyi*. Iye amakhoza kuyang'ana mmwamba. Ndipo iye amakhoza kuuluka zolimba basi momwe iye akanathera, ndipo ndi kukagunditsa mapiko ake ndi mutu pamenepo, ndi kugwera mmbuyo. Iye anagona pamenepo, ndi maso ake aakuluwo akutembenezika pamenepo, akuyang'ana mmwamba.

<sup>94</sup> “O,” ine ndinaganiza, “awo ndi amodzi mwa mawonekedwe okwiwisitsa omwe munthu akanakhoza kuyang'anapo.” Iyo ndi mbalame yammwamba. Iyo inabadwa kuti iziulukira mmiyamba. Ndipo apa, mwa kuchenjera ndi zida za munthu, iye wamangidwira khola. Iye sangakhoze. . .Iye ndi mbalame yammwamba. Iye samadziwa kanthu za pansi, nkomwe. Iye amayenera kuti azikhala mmwamba. Atagona pamenepo, akuyang'ana mmwamba kumene iye amayenera kwenikweni kuti azikakhala ali, kumene mtima wake umakhumba kuti uzikakhala, koma pali zotchinga izi pakati pa iye ndi kumeneko.

<sup>95</sup> Ine ndinaganiza awo anali mawonekedwe omvetsa chisoni, mpakana nthawi ina ine nditawona mtundu wa anthu, omwe Mulungu anawalenga mu chifanizo Chake, ataikidwa mu khola la zipembedzo ndi zinthu pomwe samakhulupirira mu



machiritso Auzimu, ataikidwa mu khola mmalo momwe iwo sakanakhoza kukhala afulu. Iwo ndi obadwira-Kumwamba. Mzimu wotumizidwa ndi Mulungu uli mwa iwo, monga choncho, koma kuikidwa mu khola umo kuti asatulukemo. Kuwaona amuna ndi akazi akuyenda mu misewu, atavala mopanda khalidwe, mu malo odyera, ataikidwa mu khola umo. Kumene, iwo amayenera kukhala ali afulu, ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Ndipo nkumamenyetsa ubongo wawo ngati utulukemo, pafupi, pa chinachake, poyesera kuti akhale afulu.

<sup>96</sup> O Mulungu, ngati ine ndikanakhala nazo mphamvu, ine ndikanati. . kapena ulamuliro, ine ndikanaigula mphungu yokalamba iyo ndikuilola iyo kuti izipita, kuilola iyo kuti izipita mwaufulu kumene iyo ikufuna kupita. Ndi chinthu choyipa, kumutchinga iye umo.

<sup>97</sup> Koma ndi zoipa bwanji izo, kuwatenga ana aamuna a Mulungu ndi kuwaika iwo mu khola ku malo kumene iwo ali. . . Kwenikweni, mzimu wawo umafuna kuti atuluke kunja uko ndi kukachita chinachake. Ndiye winawake amati, “Kulibe chinthu chotero monga machiritso Auzimu. Kulibe chinthu choterocho monga mphamvu ya Mzimu Woyera. Kulibe chinthu chotero monga *Ichi*.” Kuwaika iwo mu khola. M’bale, ndiroleni ine ndikuuzeni inu, ulipo ufulu.

<sup>98</sup> Nthawi ina bambu anagwira khwangwala wokalamba ndipo anamumanga iye, chifukwa iye anali mmunda wa chimanga. Ndipo iye. . .Ndipo mbalame zinayamba kuuluka pamwambapo, ndi kumati, “Tiyeko, Johnny Crow, tiye tipite Kummwera. Tiye tipite Kummwera. Nthawi ya chisanu ikubwera.”

<sup>99</sup> Iye anali mosauka kwambiri, iye sankakhoza nkomwe kuti ayende. Panali munthu wabwino yemwe anabwera apo, tsiku lina, ndipo anati, “Khwangwala wokalamba wosauka uyo!” Anangodula ndi kumumasulapo iye.

<sup>100</sup> Ndipo pamene iye anatero, akhwangwala enawo anabwerapo, nati, “Tiyeko, Johnny Crow, tiye tizipita Kummwera.”

<sup>101</sup> Koma i—iye anali atamangidwa motalika kwambiri, mpaka, ankangoyenda chozungulira, ndi kumati, “Ine sindingakhoze kuchita izo. Ine sindingakhoze kuchita izo.” Iye sankadziwa kuti anali atamasulidwa.

<sup>102</sup> Umo ndi momwe munthu aliri lero. Iwe sukudziwa kuti Yesu Khristu anakupanga iwe mfulu, m’bale. Tiye tichoke kwa izo. Tiye tipite kwinakwake. Mulungu anatipanga ife mfulu. Musafe ndi njala. Mulungu ali nawo madalitso achipentekoste mu milengalenga monse, n—ndi magwero osayambidwa a ubwino Wake. Tiyeni tifikire kwa izo. “Aliyense yemwe afuna, msiyeni iye adze. Msiyeni iye adze, adzamwe ku Madzi a Moyo, mwaulere.”

<sup>103</sup> Mphungu, iyo imamanga chisa chake mmwamba mu miyala. Iyo ili ngati—iyo ili ngati Mpingo. Mpingo wa Yesu Khristu ndi Mpingo umene waikidwa pa phiri, umene umapereka Kuwala. Iwo uli pamwamba. Iwo uli ndi zokhumba zapamwamba. Iwo uyenera kukhala nazo zofufuza zapamwamba, ziyembekezo, kani. Iwo uyenera kukhala ndi ziyembekezo zapamwamba, chifukwa ife takhala tikuyembekeza kuti Mulungu achite chinachake.

<sup>104</sup> Ngati inu mwabwera pano madzulo ano, ndikumanena kuti, “Chabwino, ine ndipita uko. Ngati ine nditi ndikakhale mu mzere wa pemphero, ziri bwino. Chabwino, ngati Iye ati akandiuze ine kuti ndiri bwino, ngati Ambuye akandilola ine kuti ndidziwe.” O, musakhale ndi ziyembekezo monga choncho. “Koma ngati Iye sakachita izo, ndiye ine sindikapeza kanthu.” Ziyembekezo zanu siziri zochuluka.

<sup>105</sup> Mwabwera ku tchalitchi, madzulo ano, ngati inu mukudwala, munene kuti, “Ine ndikuyembekeza kuti ndipita kwathu ndiri wabwino. Ine sindichoka ayi mpaka izo zitachitika.” Ngati inu mulibe Mzimu Woyera, munene kuti, “Ine ndikhala pano ndi kuvundira pa malo ano, kapena ine ndilandire Mzimu Woyera. Ine ndabwera pano pakati pa anthu a Mzimu Woyera. Ine ndabwera kuno kumene kuli Mzimu. Ine ndikhala pomwe pano mpaka ine nditaulandira Iwo.”

<sup>106</sup> Muzikhala momwe Buddy Robinson wakale analiri, pamene iye anafika mmunda wa chimanga. Iye anati, “Ambuye, ngati Inu simundipatsa ine Mzimu Woyera, pamene Inu muzidzabwerera padziko lapansi Inu mudzapeza mulu wa mafupa a Buddy Robinson ali pomwe pano.” Ndiyo njira yake yochitira izo. Ndizo ndendende.

Ife timazitenga izo mwachisawawa kwambiri.

<sup>107</sup> Bambo, nthawiyina, anali kuyesera kufunafuna Mulungu. Ndipo nthawi iliyonse iye akanena kuti, “Ine ndapulumsidwa,” mdierekezi amati, “Ayi, iwe suli.” Tsiku lina iye anazika chikhomo pansi. Iye anati, “Satana, kuyambira apa mpakana, ine ndiziloza kwa chikhomo ichi. Awa ndi malo pomwe ine ndinakwaniritsa zofuna za Mulungu, pomwe pano.”

<sup>108</sup> Inu muzike chikhomo chanu pansi, pambali pomwepo pamene inu mwakhala, madzulo ano, nkuti, “Satana, apa ndi pamene kukaikira kulikonse kuti kutsale. Ndipo ine ndiulukira kutali ndi Iye, madzulo ano. Ine ndivomereza ndendende zomwe Iye anandiuza ine kuti ine ndikhoza kuzichita.” Ngati inu mungazikhulupirire izo.

<sup>109</sup> Mphungu yaikulu iyi, pamene iyo ikonzeza kuti imange chisa chake, iyo imapita patali mmwamba mu miyala. Ndipo iyo imakamanga chisa chake mmwamba. Chifukwa iyo ili. . . Iyo imafuna kuti izi wateteza ana akewo.

<sup>110</sup> Umo ndi momwe Mulungu amachitira. Iye amawukwezera Mpingo Wake mu malo, ngati inu mutangomulola Iye, ndipo Iye adzakuikani inu pa malo pomwe inu muti mudzakhale kutali ndi miimba ya pa dziko lapansi. Ndithudi, Iye atero.

<sup>111</sup> Kusiñana kwake momwe ziriri kwa nkuku! Nkuku ndi mbalame, nayonso, koma iyo imamanga chisa chake ku bwalo la khola uko penapake, pansu pa dothi komwe nyenga ndi njoka, ndi china chirichonse, zikhoza kuwatenga ana ake. Iyo simadziwa kalikonse ka zammwamba. Komabe, iyo ndi mbalame; mwinamwake, m'bale wachipembedzo, koma—koma—iye ali padothi. Iye samadziwa kalikonse ka zammwamba, kuwuluka patali, kwina kwake kutali mmwamba umo komwe kuli kwa buluu ndi kokongola.

<sup>112</sup> Mayi wamkulu wa mphunguyo, pamene iye amapanga chisa chake. Momwe ine ndaziwonera izo nthawi zambiri, amapita kwina nakatenga timitengo tatikulu, ndi kutiyika ito pansu mu matanthwe amenewo. Ndi kutikokera ito cha apa ndi mulomo wake waukuluwo, ndi kuzimangirira izo pansu, ndi kutenga nthambi zaminga ndi kuzimangirira apo mozunguliza. Ndipo mkati mwa chisamo ndi mopangidwa ndi minga, makamaka, kuti amangire zooneka ngati mizati yaikulu, limodzi, yomwe iye amainyamulira pamwamba apo. Koma iye amachizika chisa chimenecho kuti sipangakhale nkuntho ungakhoze kuchikupiza icho nkuchokapo.

<sup>113</sup> Ndine wokondwa, “Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizingakhoze kuwuluka Iwo.” Thanthwe la mtundu wanji? Vumbulutso lauzimu.

“Kodi anthu amati Ine Mwana wa munthu ndine yani?”

“Ena akuti ‘Eliya,’ ena akuti ‘Mose.’”

“Koma nanga bwanji inuyo?”

Petro anati, “Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu.”

<sup>114</sup> “Wodala ndi iwe, Simoni, mwana wa Yona. Thupi ndi magazi sizinaululire izi kwa iwe. Iwe sunakaziphunzire izi mu seminare. Iwe sunaziphunzire izi ndi winawake pakukuza iwe, koma Atate Anga omwe ali Kumwamba awululira izi kwa iwe. Pa thanthwe ili ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizingaulake Iwo. Mikuntho ya moyo siidzaugwedeza Iwo.” Nchifukwa chake Iye anati Iye anali Mphungu. Iye amamanga chisa.

<sup>115</sup> Ndiye mayi mphungu wamkuluyo, pokonzekera kuti ana ake abadwe, iye amapita kunja ndipo amatenga chirichonse chomwe iye angakhoze, masamba ofewa. Iye amatenga mulomo wake waukulu ndi kuwayika iwo mu ngodya, ndi kukonza zisonga zonse, pozungulira, kuti izo zisawabaye aang'onowo. Iye amapita ndi kukatenga mwanawankhosa wake, kapena mwina kalulu, kapena chinachake, amadya nyama yakeyo; ndiye

amatenga—tsitsi, ubweya wochokera pa iyo, ndi kukakonzera chisacho. O, iye amachipanga icho mokongola kwenikweni, kuwakonzera ana ake amene akubwera.

<sup>116</sup> Umo ndi momwe Yehova Mphungu amachitira, nayenso. Iye amangozikonza izo zonse. O, mai! Pamene mwana watsopano abadwa, bwanji, mu Ufumu wa Mulungu, iye basi...Iye amaganiza kuti iye angakhoze kuyenda, koma iye nthawizonse amakhala akunjanja mmwamba ndi pansu, ndi kuthamanga chozungulira. Koma iye amakhala ali ndi nthawi yabwino. Iye ali mu chisa, chomwe chonse chiri ndi nthenga, inu mukudziwa. K—kugwa sikungamupweteke. Ndipo kotero umo ndi momwe mayi Yehova Mphungu amachitira. Iye amakonza chisa Chake mwawofuwofu kwenikweni ndi mwabwino, chifukwa cha aang'ono Ake omwe ati abadzewo.

<sup>117</sup> Pakapita kanthawi, mazira amabwera, motsatira kumabwera mphungu yaing'ono. Ndipo iye amapita mmusi uko, iye ndi abambo mphungu, ndipo iwo amawadyetsa aang'ono awo onse, mpaka iwo atafika pa usinkhu wabwino ndithu. Ndiye pamene iwo afika pa usinkhu winawake . . .

<sup>118</sup> Tsopano, mayi mphungu atsimikizira kuti mphungu izo sizidzakhala chirichonse ngati nkhuku. Ndiko kulondola. Iye samafuna kuti iwo akhale omangikira pansu. Iwo ndi mphungu, ndipo iye amadziwa kuti iwo ndi mphungu.

<sup>119</sup> Umo ndi momwe Yehova Mphungu amachitira. Iye samatifuna ife tikhale nkhuku, nkhuku za mu khola. Iye akufuna kuti ife tikhale mphungu, mmwamba mwa buluu umo, chikhalidwe cha ife nkuti tizikhala mmwamba umo kumene ife tiri afulu. “Iye amene Mwana wamupanga kukhala mfulu ali mfulu ndithudi.” Pamenepo, amawafuna iwo pamwamba apo. Kotero, masiku angapo . . .

<sup>120</sup> Momwe ine ndawapenyera iwo, nthawi zochuluka kwambiri! Masiku angapo nthawi yokasulira chisa isanadze, mayi mphungu wamkuluyo amakhoza kuuka apo pambali pa chisa chimenecho. Ine ndakhalapo, masiku ambiri, mu kutentha kwa dzuwa lowala, ndikuwapenya iwo, ndipo ndimangolira ngati mwana. Mwaona, mayi mphungu wamkulu uyo, awo ndi okulirapo. Mayi mphungu ndi wamkulupo kuposa bambo mphungu. Mapiko awo ena amatambasuka mapazi fortini, kuchokera ku nsonga mpaka ku nsonga.

<sup>121</sup> Ndipo iye amakafika pamwamba apo. Iye amadzadzitukumula akuzungulira, pa chisa icho, monga *choncho*. Ndipo iye amapita kwa aang'ono awa. Iye amatambasula mapiko ake aakuluwo ndi kufuula. Ndipo pamene iye atero, nthawizina mphungu zazing'onozo zimagwera pa nsana wao. Iye amafuna kuti iwo atero. Ndi chimene iye amafuna kuti iwo achite. Ndiye iwo amadzukapo. Ndipo iye amafuula. Chifukwa? Iye akuwaphunzitsa iwo kwa liwu lake.

“Nkhosa Zanga zimalidziwa liwu Langa.”

122 Iye amafuna kuti izo zizidziwa chimene chiri pamene nthawi yofuula ibwera. Ndipo iye akufuula. O, mai! “Ine ndikufuna kuti inu mudziwe kukwera kulikonse kwa liwu langa,” iye amatero, “chifukwa pali nkankhaziwisi zambiri. Ine ndikufuna kuti inu muzidziwa kuti ndinu mphungu. Ine ndikufuna kuti inu muzilidziwa liwu la mphungu.” Amen. Aleluya! “Ine ndikufuna kuti inu muzidziwa chomwe phokoso la mphungu liri.”

123 Ndiye iye amatambasula mapiko ake aakuluwo, ndikuti, “Yang’anani kuno. Ine ndikukonzekera kuti ndikupatseni inu kuuluka kwanu kwanokha koyamba. Koma, poyamba, ine ndikufuna inu kuti muwone momwe ine ndiriri wamkulu.”

124 O, momwe ziriri zokoma izo! Mwinamwake, nthawizina, matenda amatigwetsera ife chagada, mwina chinachake, pamene ife tingakhoze kuyang’ana mmwamba ndi kuwatenga mapiko awiri aakulu awo a Yehova, Chipangano Chakale ndi Chatsopano, ndi kuti, “Momwe Inu muliri wamkulu! Momwe Inu muliri wamkulu, Ambuye!”

125 O, iye amakonda kuwasonyeza iwo. “Tayang’anani kuno momwe ine ndiriri wamphamvu.” Iye amafuula, “Ili ndilo liwu langa.”

126 Ndipo mlaliki angakhoze bwanji kunena, ndiye, kuti Mphungu iyo siimafuula mofanana tsiku lirilonse, nthawi iliyonse pamene Iyo ifuula? Zedi. “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.”

127 Chipangano Chakale chinati, “Ine ndine Yehova. Ine ndinatsegula Nyanja Yofiira. Ine ndinawatulutsa ana achi Hebri mu ng’anjo ya moto. Ine ndine Iye yemwe ndinamuukitsa Mwana wa Mulungu.” Aleluya! “Ine Ndine Iye yemwe anatomiza Mzimu Woyera, pa Tsiku la Pentekoste.” Akuyang’ana kupyolera mu mapiko Ake aakulu, kodi inu simumakonda kuziwona Izo? Kodi Izo sizikusangalatsa mtima wanu?

128 Mphungu zazing’ono izo nkuti, “O, Mama, ife ndithudi tikukudalirani Inu. Ndinu wamphamvu ndi wamkulu.”

129 Ndinatuluka panja usiku wina ndi kukayang’ana mmwamba pa zobweretsa kuwala. Kuno nthawiyina pakale, ine ndinatengedwera ku Phiri la Palomar. Ndipo uko, kupyolera mu galasi, iwe umakhoza kuwona zaka handiredi ndi twente milioni za danga la kuwala. Werengerani izo, ndi mailosi angati omwe iwo ali, ndi angati. Kodi kuwala kumathamanga mofulumira chotani? Ndipo zaka handiredi ndi twente milioni za danga la kuwala, ndipo kudutsa izo kukadali miyezi, ndi nyenyezi, ndi maiko. “Momwe Inu muliri wamkulu! Momwe Inu muliri wamkulu!” Timphungu take tating’onoto tinayamba kuyang’ana pozungulira. “Momwe Inu muliri wamkulu!”

130 Apa pali duwa. Ilo linafa. Ilo linapita mu nthaka, koma apa ilo labwereranso kachiwiri. “Momwe Inu muliri wamkulu!”

131 Apa pali bambo wokalamba wosauka wokanthidwa ndi khansa yemwe ali mthunzi, ndipo pemphero lapangidwira pa iye. Chinthu chotsatira, inu mukumuwona iye, ali bambo wamkulu wa nkhope-yofiira. “Momwe Inu muliri wamkulu! Momwe Inu muliri wamkulu!”

132 Kuwona kamzimai kachikulire uko pa msewu kunja uko, wosakwanira kuti agaru angamamuyang’ane. Mulole mphamvu ya Mulungu igwire tcheru chake nthawi imodzi, iye afuula, “Momwe Inu muliri wamkulu!” Iye angayike kumbali cholemetsa chirichonse ndi tchimo lomwe silimachedwa kumufooketsa iye. Chinthu choyamba inu mukudziwa, iye ndi munthu wooneka-woyera. Iye ali uko ndi katraki ka Uthenga mkhwapa mwake, akuchita chinachake.

133 Mulole wogulitsa mowa uyo, uko cha pangodya, munthu woipa uyo, muloleni iye nthawi ina adzayang’ane mmwamba ndi kuwona. “Momwe Inu muliri wamkulu!” Mumuwone iye akusiya kugulitsa kachasu wake, kusiya kumwa ndi kusuta, ndudu zake ndi akaliwo, kusiya kunena bodza lake, ndi zina zotero. Ndipo ali ku msewu, ali nalo Baibulo mu dzanja lake, akuchitira umboni kwa ulemerero wa Mulungu, “Momwe Inu muliri wamkulu!”

134 Mumulole Mulungu adzatambasulire apo Chipangano Chake Chatsopano ndi Chakale chija pa inu, nthawi imodzi. Mudzayang’ane kupyolera mmasamba Ake ndikuwona chomwe Icho chiri. Inu mudzamva Liwu likufuula kuchokera Mmenemo, likuti, “Yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Chomwe Ine ndinawachitira iwo, Ine ndikuchitirani inu. Ndipo Ine ndine yemweyo. Ine ndine Yehova. Ine sindimasintha ayi.” Ine ndikumverera mwachipembedzo kwenikweni pakali pano. O, mai! Ndi momwe ine ndikudziwira bwino Izo. Izo ndi Choonadi.

135 Tsopano, mayiyo watsimikiza, mphungu zazing’ono izo sizidzakhala nkhuu ayi. Koma iye watsimikiza kuti izo zisadzakhale ayi. Inu mukudziwa chimene iye amachita ndiye? Iye akatha kudzitukumula chokwera ndi chotsika pa chisa apo, ndi kudzitambasula . . . Amati, “Tayang’anani kuno, okondedwa, momwe Ine ndiriri wamkulu. Mukuona apa. Inu muyenera kuti muzindidalira ine. Ine ndikutengerani inu kwinkwawe komwe inu muzikayenera kumakandalira ine.”

136 Ine ndikudziwa bwanji kuti Mulungu sanatumize anthu ena odwala muno madzulo ano, mwanjira yomweyo? Kukuikani inu pa malo pamene dokotala . . . Inu mukuti, “Ndine Mkhristu, M’bale Branham.” Ine ndikuzidziwa zimenezo. “Ndipo ine ndiri nawo Mzimu Woyera, ndipo ine ndiri pano, ndikuvutika.”

137 Inu mukudziwa bwanji kuti Yehova sakuyesera kuti akutengerani inu poti muziyang’ana kupyolera mu mapiko kuti muwone momwe iye aliri wamkulu? “Momwe Ine

ndiriri wamkulu! Ine ndikuchitirani inu chinachake, kuti inu muzindidalira Ine.” Ndi inu apo. “Ndipo ine ndikufuna kuti inu mudziwe chomwe inu mukuchidalirachi, poyamba. Mukuwaona mapiko Anga aakuluwa?”

<sup>138</sup> Ndiye, pakapita masiku pang’ono, inu mukudziwa chomwe mayi uyo amachita? Malingana ngati kama uyo ali atapangidwa wofewa, mphungu zazing’ono zokulirapo izo sizimafuna kuti zichokepo. Kulondola. Inu mukudziwa chimene iye amachita? Ndiye iye amafika umo momwe, ndipo amatenga mulomo wake ndi kuphwasula chidutswa chirichonse cha ubweya uwo kuuchotsa apo, ndi kuuponyera iwo kunjwa kwa chisacho. Iye watsimikiza kuti iwo asazolowerane ndi dziko. Ndiko kulondola.

<sup>139</sup> Ndi chimene Mulungu amachita, nthawizina. O, inu mukuganiza za chirichonse chachikulu ndi chirichonse chabwino, ndi chirichonse. Musamaziyang’ane zimenezo. Bwanji, inu muli mailosi milioni kuchokera ku pentekoste. Anthu achipentekoste sanali kufunafuna zinthu zophweka. Iwo ankagulitsa zomwe iwo anali nazo ndipo ankazipereka kwa osauka, ndipo iwo ankapita ndi Khristu, okha. Ndipo, lero, ife tikuyenera tikhale ndi mndandanda wa ma Cadillac ife tisanakhale auzimu. Nchiani chachitika? Chinachake chalakwika, penapake.

<sup>140</sup> Ine, ndisiyeni ine nditenge njira ndi onyozeka apang’ono a Ambuye. Ine ndinayamba ndi Yesu. Ambuye, ndipyoletseni ine, pansu pa chochitika chirichonse.

<sup>141</sup> Anthu amachita mantha ndi Kubadwa kwatsopano. Ndilo lomwe liri vuto. Iwo amachita mantha kuti abadwe kachiwiri.

<sup>142</sup> Aliyense akudziwa kuti kubadwa kulikonse, ine sindikusamala kaya ndi kuti, iko ndi nyansi. Ngati iko kuli mu khola la nkumba, kapena ngati iko kuli mu mulu wa manyowa, kapena ngati iko kuli mu chipinda cha chipatala chokongoletsedwa ndi pinki, kubadwa ndi nyansi. Ndipo anthu samafuna kukhala anyansi.

<sup>143</sup> Koma, ine ndikukuuzani inu, ine sindikufuna ndikomane ndi Mulungu mwa gawo langa. Ine ndikufuna kuti ndidzakomane ndi Kubadwa kwatsopano pa muyezo wa Mulungu. Ine sindikusamala ngati ndichita kulira, kukuwa, kuyankhula mu malirime, chirichonse chimene ine chiri choti ndichichite. Ine sindikusamala kaya ndi oyandikana nawo angati atayankhule za ine. Ndisiyeni ine ndibadwe kachiwiri.

<sup>144</sup> Ine sindikusamala kaya ndi chikhalidwe cha mtundu wanji chomwe icho chingakhale, ngati ine ndichita kuwononga kutchuka konse. Ine ndiribe kulikonse, mulimonse. Ndi chinthu chimodzi ine ndinalibe kuti ndichisiye. Ine ndinalibe kupambana kapena kutchuka. Ine ndinali basi wokhala ku phiri, pachiyambi pomwe, kotero ine ndinalibe kalikonse. Koma

i—i—ine sindikusamala chomwe icho chiri, ndine wokonzeka kuti nditaye chirichonse ndi kukhala chitsiru chifukwa cha Ufumu wa Mulungu. Inu mukafuna kunditcha ine, “Woyera-wodzigudubuza, kapena wazamizimu, kapena mdierekezi, kapena wowerenga-maganizo.” Ine sindikusamala chomwe iwo anena.

<sup>145</sup> Ine ndikumufuna Yesu. Ndicho chofunikira changa chachikulu. Pa muyezo womwe izo ziri, ine sindikusamala. Ine ndikufuna kuti ndizikomana naye Iye pa muyezo Wake; osati pa, chomwe ine ndikuganiza kuti ndi cholondola, kapena chimene winawake akunena kuti ndi kulondola. Ine ndikufuna chimene Mulungu akuti ndi cholondola. Ndi chimenecho. Ngati Iye anati, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse,” ine ndikufuna ndizimuwona Iye pa muyezo umenewo. Ngati ine ndichita kuti ndizilalikira kwa mulu wa nsanamira, ndi kumadya zigumu, ndi kumamwa madzi a mngalande, ine ndikuufunabe Uthenga. Ine ndikumufuna Khristu pa muyezo umene Khristu angadzere.

<sup>146</sup> Iye amafika pamenepo ndi kuponyera kunja kufewa konse uko. Nthawi iliyonse yomwe timphungu tating’ono ito timayamba kuti tikhale pansi, ito timakhala tiri pa minga. Pamakhala ngati pakulasa. Iye . . .

<sup>147</sup> Ndi zimenezo. Musiyeni mdierekezi, bola ngati iwo ali pafupi . . . “O, kodi inu munapulumsidwa usiku watha?”

“Inde. A-nha. Inde. Ine ndinatero.”

“Ndicho . . . O, ndine wokondwa kwambiri chifukwa cha izo.”

<sup>148</sup> Koma, inu mukayamba kukhala moyo, amanena molunjika, “Oyera-odzigudubuza! *Zakuti-ndi-zakuti!* O, ine ndadziwa gulu lomwe inu muli nalo.” Mwaona?

<sup>149</sup> Iye amakulolani inu kuti muzibayidwa, kamodzi mu kanthawi. Iye sakufuna kuti inu muzolowerane ndi dziko lino, inu mukuona. Iye akufuna kuti inu mukhale . . .

<sup>150</sup> Mayi uyo sakuzifuna nkhuu izo . . . mphungu izo kuti zidzakhale konse nkhuu. Iye akufuna kuti izo zichokemo mu chisa icho. Ziribe kanthu ngati izo ziri mu thanthwe, kapena komwe izo ziri, iye ali ndi chinachake chabwinoko kwa izo.

<sup>151</sup> Mulungu ali nacho chinachake chabwinoko kwa Mpingo. Musangokhala pansi, “Ndine wa Chipentekoste.”

<sup>152</sup> Winawake ananena, nthawiyina, anati, “M’bale Branham . . .” Bambo wachikulire uko mu Arkansas, iye anali atachiritsidwa. Iye anali akuyendayenda tsiku lotsatira ndi ndodo zake. Iye anakhala akugulitsa mapensulo pa msewu, kwa zaka ndi zaka. Akuyendayenda, ndi chikwangwani chachikulu, “Ine sindikuzifuna izi panonso, kuyambira pamene Yesu anabwera kwa ine,” kumapita akuzungulira. Ndipo usiku



umenewo, iye anali ataimirira mwa omvetsera, ndi pafupi monga *chonchi*, ku Chinyumba choyankhuliramo cha Robinson Memorial ku Little Rock. Ndipo iye anati, “Miniti yokha, M’bale Branham,” (pamene ine ndinali ndikulalikira). Iye anati, “Miniti yokha.” Anati, “Inu mukudziwa, pamene inu mumalalikira. . .” Iye anali wachi Nazarene. Iye anati, “Inu mukudziwa, inu mumalalikira basi ngati wachi Nazarene. Ndiyeno ine ndinazindikira anthu ambiri pano kuti ndi Achipentekoste. Ndipo tsopano wina akundiiza ine kuti ndinu wachi Baptisti. Ine sindikuzimvetsa izo.”

153 “O,” ine ndinati, “izo nzophweka. Ndine wa Chipentekoste Mnazarene wa Baptisti.” Ndizo ndendende basi izo. Inde, bwana. O, m’bale, zidindo zimenezo!

154 Ine ndinkakonda kukakhala apo, pamene ife tinkazitengera ng’ombe pamwamba mmapiri, ndi bondo langa nditapingasitsa pa nyanga zachikalezo apo, ndikumupenya wolondera zinyama uyo akuzipenyetsa ng’ombe izo zikamadutsa apo. Zathu zinali Tripod. Za a Grime, kumtunda uko, zinali Diamond T-Bar. Zambiri za izo za ku makola osiyana ziri ndi zidindo zosiyana zinali kudutsapo. Wolondera zinyama sankapereka chidwi kwambiri kwa chidindo. Iye ankayang’ana chisonyezo cha magazi.

155 Ameni. Ndicho chimene Mulungu ati adzayang’ane. Iye akuyang’ana kachisonyezo ka Magazi. Iye sakusamala kuti inu muli ndi chidindo chotani pa inu. Bwanji? (Panalibe ikanapita mu msipu uwo koma ya mtundu weniweni wa Hereford.) Ndipo palibe kanthu kangati kakalowe ku zipata za Kumwamba koma wobadwa-kachiwiri, kupyolera mu Magazi a Yesu Khristu. Ine sindikusamala zomwe inu mumachita, kaya ndinu aluntha motani, kapena ndinu mlaliki wabwino motani, kapena ndinu membala wa mpingo wabwino motani. Kupatula ngati inu mutabadwa kupyolera mu Magazi a Yesu Khristu, muli ndi chisonyezo cha Magazi pa inu, inu simudzalowa konse umo. Ndizo basi zonse zomwe ziripo kwa izo. “Pamene Ine ndiwona Magazi, Ine ndidzadutsa pa inu.” Ndizo zonse. Iye adzakulolani inu kuti mulowemo pamene chisonyezo cha Magazi chiri cholondola. Mulungu adzapenya Magazi a Mwana Wake Yemwe pa Mpingo.

156 Mayi mphungu wokalamba uyu, iye amatipenyenerera timphungu tating’ono ito, o, nthawi iliyonse. Ito sitimakhoza kukhala pansu. Zikungokhala ziri paliponse. Pali basi minga, minga, minga.

157 Tsopano, pali chinachake chomwe chiyenera kuti chichitidwe ndi Mpingo wa Chipentekoste uwo mu chisa chimenecho, kotero kuti iwo asakhale omangidwira mchisa. Izo nzabwino. Tsopano, ine sindiri kumenya motsutsa mabungwe. Tsopano musatengere izo mmalingaliro anu. Koma, ine

ndikuyesera kunena kuti, musati mulole kuti awo akhale malo anu olekezera. Inu muli bwino. Ine ndimawakonda mabungwe. Ndine wa mu lirilonse la iwo. Mukuona? Zedi, ine ndiri. Inde, bwana. Ine ndinabadwira mwa ilo. Aliyense ali mu mpingo; ine ndinabadwira mmenemo. Koma basi musangolekezera apo, basi musangolekezera pa bungwe ilo. Pitiriranibe ndi Mulungu, mpaka inu—mpaka inu mutakafika uko ku kuuluka kwa nokha.

<sup>158</sup> Tsopano, chinthu choyamba inu mukudziwa, pamene mayi wamkuluyo alingalira kuti, akawapatse ana ake chowachitikira chaching'ono. Tsopano, iwo ajowina mpingo ndi chirichonse kukhala chiri bwino, koma zikuyamba kubaya. Pali chinachake chalagwika. Ndiye mayi wamkuluyo amabwera pamene po patsogolo pa chisacho, tsiku lina. Iye amayang'ana pa tinthu tating'ono ito bwinobwino, ndipo pali nthenga zosalimba zambiri pa ito. Iye amadziwa kuti ngati iye atitengera tiwana tating'ono ito mu mlengalenga umo, ndi nthenga zosalimba izo, iwo akathyola makosi awo.

<sup>159</sup> Ndipo ine ndikukuuzani inu, ngati mpingo wa Chipentekoste sukhalala ndi kuyeretsedwa kwabwino, iwo athyola makosi awo, nawonso. Inu muzingokumbukira zimenezo. Pali nthenga zochulukira kwambiri zosalimba. Ndi lomwe liri vuto.

<sup>160</sup> Inu mukudziwa chimene iye amachita? Iye amakwela mmwamba pa chisacho, ndipo iye amatenga mapiko ake aakuluwo ndi kuyamba kumawakupiza iwo monga *choncho*. O, inu simunayambe mwayimapo kumbuyo kwa ndege kale, mpaka, inu mutapeza, nthenga zosalimba zikuulukira njira iliyonse pamene mphepo ya nkokomo wamphamvu iyo iyamba kusesa kudutsa mu nthenga za tiana tating'ono ito.

<sup>161</sup> Ine ndikukuuzani inu, mpingo ukusowa kugwedeza kwa chisa lero, ndi Mphepo ya nkokomo wamphamvu, kuti atengere chidziko chonse chichoke mu mpingo wa Chipentekoste, komwe iwo angamachite mwaokha. Iye tikusowa Uthenga wina wa nthawi-yachikale, wa chitsitsimutso chotumizidwa, cha Mzimu Woyera, chobadwa ndi Mulungu. Ndiko ndendende kulondola. Iye sitikusowa purezidenti watsopano; ife tiri naye wina, wabwino. Iye sitikusowa watsopano, mameya atsopano a mzinda, chirichonse. Sindizo ayi. . . Iyo ndi ntchito yawo. Koma chimene ife tikusowa, ngati atumiki, ndi kumalalikira Uthenga ndi kuubweretsa mpingo kubwerera ku pentekoste kachiwiri, kuubweretsa iwo ubwerere ku chowachitikira cha mphungu kachiwiri. Ndicho chomwe mpingo ukusowa. Ndizo, o, basi. . . Inu simukufuna kuti mukhale nkuku. Ndinu mphungu. Inu muyenera kuti muzidya Chakudya cha mphungu.

<sup>162</sup> Ndipo uyu anali apa, atakhala pamene po, akuthotholapo nthenga zonse zakale zazing'ono izo. Chifukwa, ngati iye satero, ito. . . Ngati iwo satero, iwo sakhala ndi nthenga zokwanira

zitatsalire kuti awuluke. Iye sawatenga iwo mpaka nthenga zonse izo zakale zazing'ono za ukhanda zitauluzika pa iwo.

<sup>163</sup> Ndiye iye amabwera pamwamba apo, ndipo iye amafuula. Iye wakonzeka kuti awapatse iwo chowachitikira china ndiye. Iye amawatambasula mapiko ake okula mapazi fortini monga choncho. Timphungu tating'ono ito timafikirapo, timakwerapo. Iye akuyankhula kwa iwo apo, chifukwa iwo amva liwu lake. Iwo akudziwa kuti azimudalira iye apo, momwe angaulukire. Iye akunena—kuti, “Tsopano, ana, ine ndikuti ndikutengereni inu kokauluka mwanokha.” Aliyense akupita apo, ndipo akutenga phazi lake laling'onolo, ndi kuligwiritsa mu phikolo, akuika mulomo wake waung'onowo molumitsa imodzi ya nthenga zimenezo. Bwanji, izo sizingakhoze kuthothokamo. Iyo ingatenge mphungu fifite, mwa mphamvu za nthenga zimenezo mu phiko lake. Ndipo iye akuwagwiritsa mowayala mu nthengamo monga *choncho*, ndipo mayi wamkuluyo akukweza mapiko ake monga *choncho*, nkuuluka kuchoka pa thanthwelo.

<sup>164</sup> Apa iye akupita, kukwera mmwamba, mmwamba, mmwamba, mpaka iye amafika kutali mmwamba mwa buluu, patali kwambiri. Ana aang'ono awo sanayambe afikako uko kale. O, iwo akungokhala nayo nthawi yodabwitsa iyo.

<sup>165</sup> Chinthu choyamba, inu mukudziwa, inu mukudziwa chimene iye amachita? Amatembenuka chagada kumene ndi kuwasasa iwo, aliyense, achokepo. Iwo ndi mphungu. Iwo ayenera kumadziwa kaulukidwe kake. Ndiko kulondola ndendende. Iye amawasasa iwo, akhale okha. Chabwino, ana ena aang'ono awo. . . Iye amafuula, “Chabwino, ananu, ndinu mphungu. Ziulukani.”

<sup>166</sup> Utali wonse womwe inu muziti, “Chabwino, ine ndine wa mu mpingo *uwu*. Ine ndikukuuzani inu. Ine sindikudziwa za *Izo*.” Inu simudzauluka konse. U-nhu. U-nhu. Chabwino. Inu mukusowa mudzasasidwepo nthawi ina, mu mlengalenga umo.

<sup>167</sup> Mphungu zazing'ono izo zikayamba kuuluka. Iye amafuula, “Zikupizani mapiko anu, ananu. Muzingomakupiza chikhulupiriro chanu chochepacho, mmwamba ndi pansi. Inu muli mmwamba mokwanira tsopano moti inu simuligunda dothi.” Inu mukudziwa chiani? Ndiye chimene iye amachita, iye amathawira ku mbali imodzi, kuti azikawapenyera iwo. Iye amayandama mozungulira pamenepo. Ndipo apa iwo ali, basi—ndendende basi monga chitsitsimutso cha Chipentekoste, basi pidigu pidigu, wina pa mzake, wina, kumangokupiza, mwa zonse zomwe iwo angakhoze kuzichita. Iwo samasamala. Iwo ali ndi chidaliro chapamwamba mwa mayi wawo ali pamwamba apoyo akuwapenyera iwo.

<sup>168</sup> Kodi mpingo uyenera uzichita izo motani? Ngati imodzi ya mphungu, zazing'ono izo, zichita chizungulire, iye amasesera

pansi ndi mapiko aakulu awo ndi kukamunyamula iye mmwamba, ndi kumutengeranso iye mu chisomo kachiwiri. Tsopano, uko sikuphunzitsa kwa Baptisti. Ilo ndi Baibulo. Kotero, izo zimamubweretsa iye kubwerera mmwamba kachiwiri. Amamusasanso iye kachiwiri; kumulola iye kuti ayambire katsopano. Amen.

<sup>169</sup> Mphungu izo ziri ndi chidaliro mwa mayi wawo, chidaliro chapamwamba, kuti mayiyo awathandiza iwo ndi kuwanyamulira iwo mmwamba kachiwiri. Kuwanyamula iwo pa mapiko a mphungu, ndi kuwatengera iwo mmwamba umo ndi kukawasasa iwo kachiwiri. Kumulola iye ayambire kachiwiri. Ngati inu. . .

<sup>170</sup> “Ngati ine ndigwa kapena ngati ine ndilephera, mundirole ine ndiwuke ndipo ndiyesere kachiwiri, O Ambuye.” Pitani kachiwiri. Mulungu akukwezerani inu pamwamba pomwe aponso, kukutengerani inu pamwamba apo ndi kukakusasani inu mokutayani kachiwiri. Ziyesera kudziyandamitsa wekha, ndi kumangopitirira choncho. Uzingopitirira kukupiza mpaka iwe utaphunzira kuuluka. O, mai! Nkhuku yaikulu yosaukayo siimadziwa kanthu ka izo. Iye samadziwa kanthu ka izo, chifukwa iye sanayambe wakhlapo mmwamba umo; palibe alifonse a makolo ake anafikapo mmwamba umo. Zonse zomwe iye amadziwa ndi kujowina mpingo ndi kumakhala pansi, mwaona, mu bwalo la khola. Iye samadziwa zambiri za izo.

<sup>171</sup> Nthawi ina mwamuna anali kuutamiritsa nkhuku, ndipo iye sankakhoza kupeza mazira okwanira. Kotero iye anachipeza chisa cha mphungu, ndipo anakwera pamwambapo ndipo anakatenga dzira la mphungu ndi kukaliyika ilo pansi pa nkhukuyo. Ndipo pamene gulu ilo la tofungatiridwato tinakonkhomoledwa, mphungu iyo inali kanthu kakang’ono kowoneka-moseketsa, kwa nkhuku zina izo.

<sup>172</sup> Umo ndi basi momwe Iwo umabwerera, mmodzi pa kufungatiridwa kulikonse. Basi ndi momwe izo zimachitikira. Izo ndi zoon. Ndipo apa iye anali, kanthu kakang’ono kowoneka-moseketsa.

<sup>173</sup> Iye sankakhoza kumvetsa kuluku wa nkhuku, nkhuku yaikuluyo uko m—mu mulu wa manyowa panja, “Ife tikhala ndi chakudya chachisangalalo usikuuno. Ife tikachita zonse *izi*, monga choncho. Kuluku, kuluku, kuluku. Masiku a zozizwitsa anapita. Palibepo chinthu chotero ngati machiritso Auzimu. Kuluku, kuluku, kuluku, kuluku.” Kumadya zinthu zonyansa izo za maphwando a bunco akale, ndi masewero, ndipo atavula zovala zawo, ndi chirichonse monga choncho, matelevizioni ndi mtundu wonse uwo wa zachabechabe.

<sup>174</sup> Mwana wamng’ono uyo anali mphungu. Izo sizimakhazikika ndi iye. Izo zinkamupangitsa iye kusanza, kuzinunkhiza izo. Iye amati, “Mai, ine sindidzakwanitsa konse izo.” Kumayenda

akuzungulira, mai, iye anali mnyamata wamng'ono wowoneka-moseketsa.

175 Iwo anati, “O, tiyeko, wokondedwa. Ife tikhala ndi phwando lalikulu, usikuuno. Ife tikatumikira.”

176 Iye sankafuna kalikonse ka zinthu izo. Iye ankayenda kuzungulira uko ndipo ankawona. “Chiyani? Ine ndine bakha wooneka-mosamvetseka pano.”

177 Ndipo ine ndikukuuzani inu chinthu chimodzi, m'bale, pamene mwamuna abadwa kuti akhale mwana wa Mulungu, tizikhulupiriro takale ndi zipembedzo sizingakhoze konse kumukhutitsa iye. Ayi, bwana. Zinthu za mdziko, masewero a basketball, ndi maphwando, n—ndi masewero a bunco, ndi mitundu yonse ya zosangalatsa izi zomwe mipingo yamakono ikuzichita lero mu tsiku lathuli. Palibe zodabwitsa, iwo akugwirizana, “Mulungu ali kuti?” Iwo amukwiyitsira Mulungu kutali ndi iwo. Ndizo ndendende kulondola. Inde, bwana. Nkhuku zimakonda zinthu za mtundu umenewo, koma mphungu sizitero. Icho si chakudya cha mphungu.

178 Apa iye amayenda, akuzungulira pamenepo. Ndipo, mai, zonse...zonse izo zikuyang'ana apo. Izo zonse zinali zitathamangira ku malo *awa*. Basi...Iye amakhoza kupalasa zinthu zina zowoneka-mwanyansi, ndipo izo zimathamangira apo ndi kumakadya izo. Unhu! “O, tiyeko, tiyeko, jowinana ndi ife.”

179 Koma iye ndi munthu wodzilekanitsa. Inde, bwana. Iye sankafuna chirichonse cha zinthu zimenezo. Izo sizinkawoneka bwino kwa iye. Sizinkanunkhira bwino. Zinalibe chikhalidwe cha mtundu wolondola pozungulira apo. Iye sankazikonda izo, nkomwe. Iye anati, “Ayi, ayi.”

180 Ndipo tsiku lina, mayi mphungu wachikulire anabwera akumusaka iye. (Ndine wokondwa kwambiri kuti Iye anandidzera ine.) Iye anaulukira pa khola ilo, kuti ayang'ane pansi apo, ndipo iye anamuona mwana wakeyo. Ndipo iye anafuula. Iye anati, “Wokondedwa, iwe si nkhuku. Ndiwe wanga.” Pamene iye anamva liwu limenelo, iye anayang'ana mmwamba. Izo zinkamveka bwino. Chikhalidwe chake chinali mphungu. Chikhalidwe chake.

“Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.”

“Ameni,” iye anayankha mofuula.

181 “Musalikonde dziko kapena zinthu za mdziko; ngati inu mutero, chikondi cha Mulungu sichiri mwa inu.”

“Ameni,” iye anati. “Izo zikumveka bwino.”

182 “Ine ndikabwerera kumeneko, wokondedwa, iwe ukhoza kulumpha. Chinthu chokha chimene iwe uyenera kuti udzachite ndi kukupiza mapiko ako aang'ono a chikhulupiriro. Iwo adzakunyamula iwe.”

“Ine ndichokamo bwanji muno, amayi?”

<sup>183</sup> “Ingokupiza mapiko ako. Ndizo zonse. Iwe ubwera bwino bwino. Ingotenga chikhulupiriro chako ndi kukwera pa icho. Uyambe kupita mmwamba, chifukwa iwe ndiwe mphungu, kuyamba ndi kuyamba. Zedi. Ndiwe mphungu, kuyamba ndi kuyamba. Zikupiza mapiko akowo.” Iye anali kuyandama akuzungulira, pamwambapo. “Iwe ukuwoneka ngati mmodzi wa anga pansi apo, pomwe iwe ulipo.”

<sup>184</sup> Ndipo mwana wamng’ono analumpha pa mapazi ake, ananjanja mmwamba ndi pansi, nthawi zinai kapena zisanu, inu mukudziwa, kukhala ngati akuwombetsa manja ake aang’ono, kapena mapikowo, palimodzi, monga choncho. Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, iye ananyamutsa mapazi ake kuchoka pa nthaka.

<sup>185</sup> Koma inu mukudziwa zomwe iye anachita? Mphungu yaing’ono iyi, iye anakakhala pansi pamwamba pa mtengo pomwe apo mu kholalo, pakati pomwe pa chipembedzo chachikulu cha Chipentekoste. Inu mukudziwa chiani? Mayi mphungu anauluka mozungulira kachiwiri. Iye anayang’ana pa iye, atavala mathalauza, tsitsi lodulidwa, nkhope yopentedwa. Anati, “Wokonedwa, iwe ukuwoneka mochuluka ngati khwangwala wa chipentekoste kuposa momwe uliri mphungu ya chipentekoste. Iwe usowa kuti udzisukusulitse wekha mochuluka pang’ono kuposa choncho, kapena ine sindingakhoze konse kukutenga iwe.” Kulondola.

<sup>186</sup> Ine sindikutanthauza kuti ndipweteketse kumverera kwanu, koma ine ndikufuna kuti ndimete chinachake chichoke pa inu. Ndiroleni ine ndikuuzeni inu, m’bale. Chifukwa, mpingo wa Chipentekoste ukusowa kuyeretsedwa, kuchokera paguwa mpaka ku mipando, ndiko kulondola ndendende, kuika kumbali zolemetsa. Palibe chodabwitsa kuti ife sitingakhoze kukhala ndi chitsitsimutso, tikumadya zinthu za miimba, kumatsala pakhomo usiku kuti tiziwonera zina za televizioni zozikonda mmalo momapita ku msonkhano wamapemphero. Kumavala zakale izi. . . Akazi kumavala zovala izi, ndi amuna kumamwa chakakumwa pang’ono, kosangalatsa, ndi kumanena nthabwala zoipa ndi zinthu pakati pa wina ndi mzake. Inu mukutanthauza chiani, amuna? Mulungu sangakhoze kufikira mu nyansi za zinthu ngati zimenezo.

<sup>187</sup> Inu mukhoza kukhala ndi mipingo yaikulu kwambiri yomwe ilipo mu dzikolo. Inu mukhoza kukhala ndi ndalama zambiri kuposa zomwe inu munayamba mwakhalapo nazo. Izo ziribe kanthu kamodzi kochita ndi izo. Inu mukhoza kumayanjana ndi zomwe inu mumazitcha gulu laluntha labwinoko. Inu mukhoza kumavala suti yabwinoko ya zovala, koma, m’bale, Mulungu akufuna mtima woyera ndi manja oyera. Iye akufuna mpingo wotsukidwa, ndiye Iye akhoza kudzisonyeza Yekha.

188 Pamene Mulungu atambasula apo mapiko Ake aakuluwo ndi kusonyeza mphamvu Yake, kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, mphungu imati, “Inde, Ambuye. Ndi chimene ine ndikuchifuna. Ine ndikumenyera chimenecho. Ine ndikubwera kwa icho.” Zedi. Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

189 Mai, kodi nthawi yathu yapita kuti? I—ine ndikungomverera ngati ndizilalikira tsopano. Ine basi...Koma—koma ife... Kuti?

190 O! Chomwe mpingo wa Chipentekoste ukusowa ndi kuyeretsewa. Iwo ukusowa kuskusulitsidwa. Iwo ukusowa kukhulidwa, kuyeretsewa. Anthunu, inu si a mdziko. Inu musamadzifanizire nokha ngati anthu ena. Musamayesere kumadzifanizitsa nokha ndi akatswiri ena akanema. Ndinu mwana wamkazi wa Mulungu. Ndinu mwana wamwamuna wa Mulungu. Musati muziyesera kukhala ngati Matt Dillion kapena winawake. Musati muziyesera kukhala ngati Peabody Ernie, kapena chirichonse chomwe dzina lake liri, kapena ena a amuna amenewo. Inu simuli ayi... [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] “Musamakonde zinthu za mdziko. Ngati inu muzilikonda dziko, kapena zinthu za mdziko, chikondi cha Mulungu sichiri nkomwe mwa inu.” Ine ndikudziwa, m’bale, izo nzodwalitsa. Izo zikukupangitsani inu kudwala.

191 Amayi anga aang’ono okalamba akummwera anakonda kundiuza ine zimenezo. Ana tonse aang’ono ife tinkabwera usiku Loweruka, ndi mtsuko waukulu wakale wa nkunguza, ndipo iye ankatsanulira madzi mmenemo, n—ndi kumawasambitsa anawo. Ndipo ine ndinali wotsirizira pa khumiwo. Ndipo ine ndinkasamba motsirizira mu mtsuko womwewo wa madzi, ankangowatenthetsa iwo pang’ono pokha. Ndiyeno amayi ankatenga... Ife tinali osauka kwambiri, ife... .

192 Iye ankatenga zikopa za nyama yakale ndi kuziyenga izo, kuti apeze—mafuta kuchokera mwa izo. Ife sitinali kukwanitsa kugula mafuta ophikira, ndipo koteri iwo ankapeza mafuta kuchokera mmenemo, kuti aziwayika pa chigumu cha chimanga. Ndipo ife tinali ndi nandolo wangati maso-akuda, masamba a tanaposi, ndi chigumu cha chimanga. Ndi—ndipo ife tinkatenga zi... .

193 Ife tinali kuwengedwa ndi zinthu, ndipo amayi, usiku wa Loweruka lirilonse, ankatipatsa ife kuti timwe mafuta a msasi. I—ine sindinkakhoza nkomwe kupirira ndi zinthu izo apobe, fungo lake. Ndipo ine ndimakhoza kubwera kwa iwo, nditagwira mphuno zanga. Ine ndinkati, “Amayi, musatero, musatero, musatero. Ine sindikukhoza basi kupirira nazo.”

194 Iwo anandipatsa ine mawu abwino. Anati, “Mwana, ngati iwo sakupangitsa iwe kuipidwa, iwo sakuchitira iwe ubwino uliwonse.”

<sup>195</sup> Umo ndi momwe ziriri ndi kulalikirira, Mawu awa. Ngati Iwo sakuipirani inu, bwino bwino, kuti apangitse zauzimu zanu kuyamba kumagwira ntchito, iwo sangakuchitireni inu ubwino uliwonse. Ndiko kulondola. Mawu amakupanga iwe kukhala mfulu, ndipo mfulu ndithu, kudula maunyolo. Kodi inu mukuzikhulupirira zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

<sup>196</sup> Mpingo ukusowa chitsitsimutso cha Mzimu Woyera. Iwo ukusowa kusesa kwa mnyumba. Izi ndi mphungu. Musazidyetse izo chakudya cha nkukhu. Izo ndi mphungu. Zifikitseni izo kunjira uko kumene izo ziyenera kuti zizikauluka kapena zifa. Ndizo zonse. Ndipo Mulungu aziyang’anira pa chuma Chake. Iye sali konse kutali kwambiri. Iye nthawizonse amakhala ali pafupi, kuti akunyamulireni inu mmwamba. Kodi inu mukuzikhulupirira izo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu ndiye kwa mawu a pemphero.

<sup>197</sup> Ndi angati akufuna kuti akumbukiridwe tsopano? Ndikuti, “Ambuye, chitirani chifundo kwa ine. Ndipatseni ine maganizo a mphungu. Ndipatseni ine zokhumba za mphungu. Ndipatseni ine moyo wa mphungu. Ndiloleni ine ndiziuluka mwa buluu Mwanu kutaliko, Ambuye, kumene zinthu zonse ziri zotheka kwa iwo amene akhulupirira. Pangani chikhulupiriro mwa ine. Aloleni mapiko anga akule. Aloleni akatumba anga, kuzungulira mwapiko anga, akule mpaka ine ndizikhoza kumamuwona kwanikweni Yesu.” O, Mulungu akudalitseni inu.

<sup>198</sup> Atate Akumwamba, o, u—Uthenga ukhoza kumveka motsutsa, Ambuye, koma iwo sumatanthauzidwa mwa njira imeneyo. Izo zinangokhala mwanjira yaing’ono, yokha yomwe ine ndiri nayo yowalolera anthu kuti azidziwe, Ambuye, chomwe, chimene ine ndikukhulupirira, kuti Inu mukuyesera kuti muchifikitse kwa iwo, kuti muugwedeze mpingo. Chuma Chanu chachikulu ichi, mpingo wawukulu wa Chipentekoste uwu, mpingo waukulu, momwe iwo ulirimu; Inu mwagwedezera mitundu yonse ya mphatso powazungulira iwo, mitundu yonse ya zizindikiro ndi zodabwitsa, ndipo iwo akumakhala kumbuyo komweko, ngati nkukhu, nthawizina. O Mulungu, aloleni iwo awone kuti iwo ndi mphungu. Iwo akhoza kuuluka, kungotenga chikhulupiriro chawo ndi kuuluka kuchoka kwa izo, achokeko ku mayankhulidwe akale awa akuti, “Izo sizingakhoze kuchitika. Palibe kanthu kwa izo.” O Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu mumudalitse aliyense muno madzulo ano, ndipo mulole aliyense wa iwo afungatiridwe moyandikirana pansu pa mapiko a Yehova. Perekani izi, Atate. Ine ndikuwapereka iwo kwa Inu, mu Dzina la Yesu, Mwana Wanu. Ameni.



199 Izo ziri kwa Ambuye Mulungu, zomwe Iye ati achite. Tsopano ife tikhala ndi mzere wa pemphero, kuti ife tikhoze kutulukamo muno. Ine ndikufuna kuti inu mupite ku tchalitchi, usikuuno. Mulungu akudalitseni inu. Inu mukuwakonda Ambuye? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Ameni.

200 Tiyeni tingoimba nthawi imodzi ina, kuti ine ndikhoze kuimva iyo mu Tulsa, mu gulu lalikulu ili.

Ndinkonda Iye, ndinkonda Iye  
Poti anayamba kundikonda,  
Nagula chipulumutso changa  
Pa Kalvare.

201 Chabwino. “Ine . . .” Tiyeni tiipange iyo kumvekera bwino tsopano, kwa Iye. Uthenga watha. Tiyeni tizingomupembedza Iye.

Ndinkonda Iye,  
Poti anayamba kundikonda  
Nagula chipulumutso changa  
Pa Kalvare.

202 Tsopani tiyeni tingokhala ngati tikuweramitsa mitu yathu, ndi kukweza manja athu, pamene unyinjira ukukhala chete tsopano.

Ndinkonda Iye, ndinkonda Iye  
Fupikirani, Ambuye.  
Poti Iye anayamba kundikonda  
Nagula chipulumutso changa  
Pa mtengo wa Kalvare.

[M’bale Branham akuyamba kung’ung’uza *Ndinkonda Iye*—Mkonzi.]

203 Anali chiani awo, handiredi kapena fifite? Fifite? Inu amene muli ndi khadi la pemphero nambala wani, kwezani mmwamba dzanja lanu. Imirirani ku mapazi anu ngati inu mungathe. Khadi la pemphero nambala wani, H. H, nambala wani, kwezani mmwamba dzanja lanu. Khadi la pemphero nambala wani, kwezani mmwamba. Inu muli . . . Kodi inu ndi munthuyo, dona? H, nambala wani, bwerani pomwe pano. H, nambala thuu?

204 [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] “. . .nkhosa yotaika ya Israeli.” Ndi kulondola uko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

205 Tsopano, kodi pali mitundu ingati ya anthu pa dziko lapansi? Mitundu itatu: Anthu a Hamu, Shemu, ndi Yafeti. Tsopano, amenewo anali Myuda, Wamitundu, ndi Msamaria, yemwe ali theka Myuda ndi Wamitundu. Kodi inu mumadziwa?

206 Ndi angati akudziwa kuti Yesu anamupatsa Petro mafungulo pa Pentekoste, isanafike? Ndiko kulondola. Iye anatsegulira,

mafungulowo ku Ufumu, ku Yerusalemu, kwa Ayuda. Ndi kulondola uko?

207 Filipo anapita kwina ndipo anakawabatiza iwo, uko ku Samaria. Komabe, Mzimu Woyera nkuti usanabwere pa iwo, chifukwa, Petro anali ndi mafungulo; anabwera uko ndipo anadzaika manja ake pa iwo, ndipo iwo analandira Mzimu Woyera, Asamaria. Nkulondola uko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

208 Kuja kunyumba ya Kornelio, ndi ndani anaitanidwira uko? Petro.

209 Kuyambira apo, palibe kanthu kakunenedwa pa izo. Eya. Timibadwo tonse tinali ndi... Mitundu yonse inali nawo Uthenga utatsegukirako: Anthu a Hamu, Shemu, ndi Yafeti.

210 Tsopano, ngati inu mungazindikire, ine ndikufuna kuti inu muwone. Tsopano, panali magulu awiri a anthu, mitundu iwiri ya anthuwo, inkayembekezera Mesiya. Anali ndani ameneyo? Ndipo anali... Iwo anali Myuda ndi Msamaria. Koma, Amitundu, ife, ife tinali Angelezi-Achisaxoni. Ife tinali ndi chibonga pa nsana wathu, tikupembedza fano. Ife sitinali kuyembekezera Mesiya ayi.

211 Tsopano, ine ndikungogwira tcheru chanu, ngati ine ndingathe, mpaka m—mzere wa pemphero utakonzeka, kuti iwo onse akhale okonzeka kubwera mu mzere wawo.

212 Tsopano, ife sitinali kumuyembekezera Mesiya ayi, kotero ife sitinalandire aliyense. Kotero ndiye, koma, tsopano, kwa iwo omwe anali kumuyembekezera Iye, Iye anawonekera kwa iwo. Tsopano, ndi angati akukhulupirira zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

213 Chabwino, tsopano—tsopano, iwo atamukana kale Mesiya wao, ndiye, kumbukirani, Iye anapita kwa Ayuda. Kodi Iye anasonyeza chizindikiro cha mtundu wanji? Iye ankadziwa chinsinsi cha mtima wawo. Tsopano kodi mpingo wa Chiorthodox unati chiani za Iye? “Iye ndi Bezezebule, wambwebwe.”

214 Yesu anati, “Ine ndikukhululukirani inu chifukwa cha izo. Koma tsiku lina Mzimu Woyera udzabwera kudzachita chinthu chomwecho, ndipo, kudzayankhula moutsutsa Iwo, sizidzakhululukidwa konse mu dziko lino, ngakhale mu dziko lomwe liri nkudza.” Nkulondola uko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

215 Tsopano penyani. Iye anachita chizindikiro chimenecho pamaso pa Ayuda; Iye anachichita icho kwa Asamaria; koma osati kwa Amitundu. Inu simungapeze nkhani imodzi ya izo. Ayi, bwana. Koma Iye asanachoke... Tsopano, Iye ananena kwa mkaziyo... Tsopano mpenyeni mkazi uyu, hule uja, ife timamutcha iye.

216 Iye ankadziwa mochuluka za Mulungu kuposa theka la alaliki mu United States. Ndiko kulondola. Iwo ndi aluntha kwambiri. I—iwo alibe malo kwa chokuchitikira chazimu. Ambiri a iwo ndi Akhristu abwino, abale azauzimu, koma ena a iwo akadali nkuku.

217 Ndiye, iye anabwera pamenepo. Ndipo mkazi wamng’ono uyo...Iye anapita uko, natumiza ophunzira Ake achokepo, nakhala pansu pamenepa. Chifukwa, anthu a Chisamaria anali akufuna-...Ndi angati akudziwa kuti Asamaria ankamuyembekezera uyu, Mesiya? Inu mukukhulupirira zimenezo? Chabwino, ndiroleni ine ndikuwerengereni inu, Yohane Woyera 4, tsopano. “Mkazi anabwera ku chitsime, mkazi waku Samaria. Iye anati. . .”

218 Tsopano, pamene ine ndiri apo, kuyambira forte mpaka fifite, mu H. Forte mpaka fifite, tengani malo anu. Chabwino. H, forte mpaka fifite, awo ndi makadi onse a pemphero, atenge malo awo.

219 Tsopano zindikirani, pamene Iye anapita uko ku chitsime tsiku lijali nakakhala pansu, ndipo ophunzira anapita mu mzinda kuti akagule zitumbuwa zina. Pamene iwo anali atapita, mkazi wooneka-mokondeka anabwera akuyenda, ali ndi mtsuko pa mutu wake. Ndipo iye anatsitsira chotungira pansu, kuti atungepo madzi. Ndipo iye anamumva Winawake akuti, “Ndibweretsere Ine akumwa.” Ndiye iye anayang’ana uko, iye anawona Myuda.

220 Iye sanali wopitirira sate, koma Lemba linati Iye ankawoneka wa fifite. Ndi angati akudziwa zimenezo? “Ndiwe Mwamuna wosapitirira usinkhu wa zaka fifite, ndipo ukunena kuti Iwe unamuwona Abrahamu?”

Iye anati, “Abrahamu asanakhalepo, INE NDINE.” Ndiko kulondola.

Kotero anati, “Iwe suli pa usinkhu woposa zaka fifite.”

221 Ndipo apo iye anali, atakhala pamenepo pa chitsime. Apo panali Yesu, atakhala powonekera pa chinachake monga ichi. Ndipo Iye anati, “Ndibweretsere Ine akumwa.” Iwo anali ndi kusankhana apo, monga iwo anali nazo Kummwera, akuda ndi azungu. Iye anati. . .

222 “Si mwambo wake kuti Inu, pokhala Myuda, mundifunse ine, mkazi, Msamaria,” anati.

223 Iye anati, “Mkazi. . .” Mvetserani tsopano, chimene ine ndikukuuzani inu. Inu muziphonya izi. “Mkazi, ngati iwe ukanamudziwa Yemwe iwe ukuyankhula naye, ngati iwe ukanadziwa, Iwe ukanandifunsa Ine akumwa. Ndipo Ine ndikanakupatsa iwe madzi omwe iwe sukanamabwera kuno kudzatunga.”

Iye anati, “Chitsimechi ndi chakuya. Inu mulibe choti mutungire nacho.”

224 Ndiyeno kukambiranako kunapitirira. Kodi Iye anali kuchita chiani? Kukhudza mzimu wake. Ndi chinthu chomwecho chimene ine ndikuchichita pakali pano kwa inu, kuyesera kugwira tcheru chanu.

Iye anati, “Ndibweretsere Ine akumwa.”

225 Kukambiranako kunapitirira mpaka Iye anapeza lomwe linali vuto lake. Ndi angati akudziwa lomwe ilo linali? Iye anali akukhala mu chigololo. Koteru Iye anati, “Mkazi, pita ukamutenge mwamuna wako ndipo abwere kuno.”

Iye anati, “Ine ndiribe mwamuna aliyense.”

226 Anati, “Uko nkulondola. Iwe wakhala nawo asanu, ndipo yemwe iwe ukukhala naye si mwamuna wako.”

227 Tsopano, kodi mkazi uyo. . . pansu pa chikhalidwe chake, pokhala monga momwe ife tikuganzira. Iye, wachiwerewere, mkazi wa mbiri-yoipa, mvetsarani zomwe iye ankadziwa za Lemba. Iye sanamutche Iye monga alaliki ankachitira, “Belezebule, wambwebwe, mdierekezi.”

228 Ndipo aliyense akudziwa kuti mbwebwe ndi wa Mdierekezi. Koteru wambwebwe ndi chiyani? Ndi chinthu chosokonezeka.

229 Mdierekezi sangakhoze kulenga kalikonse. Iye, ngati iye ali mlengi, iye akhoza kudzipangira dziko. Koma iye akhoza kupotoza zomwe Mulungu analenga. Kodi inu mukumvetsa izo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Apa, apa, izo sizimamveka bwino, mwa omvetsera osakanizikana. Mwamuna akhoza kukwatira mkazi ndi kumakhala ndi iye ngati mkazi wake, ndipo pogonapo ndi posaipitsidwa. Kachitidwe komweko ndi mkazi wina, iye wapita, mwaona, ndi kupotoza chinthu chomwe chiri cholondola. Inu mukumvetsa chimene ine ndikutanthauza? Satana amapotoza.

230 Wambwebwe ndi kupotozedwa kwa mpenyi wa Mulungu, wopotozedwera mu madera a mdierekezi.

231 Ndiyeno, zindikirani, iye sanamutche Iye zimenezo. Iye anati, “Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndinu Mneneri.” Ndi angati akudziwa kuti iye ananena choncho? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Zosiyana mochulukwa kwambiri ndi zomwe alaliki awo ankanena. Anati, “Ine ndazindi—ndazindikira kuti Ndinu Mneneri.”

232 Tsopano penyani. Mvetsarani. “Ife tikudziwa. Ife Asamaria, ife tinaphunzitsidwa. Ife tikudziwa, pamene Mesiya adzadza, Iye azidzachita zinthu izi.” Kodi icho chinali chizindikiro cha Mesiya? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi chinali? [“Ameni.”] “Ife tikudziwa, kuti pamene Mesiya abwera, Iye azidzachita zinthu izi. Koma Inu ndi Ndani?”

Yesu anati, “Ine ndine Iye yemwe akuyankhula ndi iwe.”

<sup>233</sup> Iye anathamangira mu mzinda, ndipo anakawauza anthu, “Bwerani, mudzamuwone Munthu Yemwe wandiuza ine zinthu zomwe ine ndimazichita. Kodi uyu si Mesiyo?”

<sup>234</sup> Koma Iye sanazichite konse izo kwa Amitundu. Koma kodi Iye analonjezera izo kwa Amitundu? Pakuti, ife takhala nazo zaka thuu sauzande za kuphunzitsidwa, basi monga Ayuda ndi Asamaria analiri nazo, za kuphunzitsidwa, kuyembekezera Mesiya.

<sup>235</sup> Tsopano, Yesu anati, “Monga zinaliri mu masiku a Loti, mu Sodomu, chomwecho zidzakhala ziri pa Kudza kwa Mwana wa munthu.”

<sup>236</sup> Tsopano penyani. Mu masiku a Sodomu, iwo anali ndi chitsitsimutso ndi aluntha, ndi Loti. Billy Graham wamakono anapita uko ndipo anakalalikira Uthenga, anawachititsa iwo khungu. Koma penyani chomwe. . .

<sup>237</sup> Abrahamu anali Mpingo, wosankhidwa, wachipentekoste, woitanidwa-atuluke, wolekanitsidwa kwa zinthu za dziko.

<sup>238</sup> Tsopano, alipo achipentekoste mu mpingo wa Methodist. Alipo achipentekoste mu mpingo wa Baptist. Chipentekoste si chipembedzo. Ndi chokuchitikira chimene aliyense akhoza kukhala nacho, yemwe akuchifuna icho. Chipembedzo cha Chipentekoste chiribe kusankha pa Dalitso lirilonse la chipentekoste, ngati Katolika angakhoze kukhala nalo ilo. Ndinu achipentekoste chifukwa inu muli ndi Dalitso la chipentekoste mu mtima mwanu.

<sup>239</sup> Koteru, Abrahamu anali woitanidwa-atuluke, ndipo Mngelo uyu amene anali uko ndi Abrahamu. Ndipo Mngeloyo atapita. . . Iye anamutcha Iye, “Ambuye.” Elohim. Ndi angati akudziwa kuti Elohim anali Mulungu Yehova wamkulu? Zedi. Ambuye Mulungu, ndipo Iye anakhala ali ndi nsana Wake utatembenuzidwira ku hema. Penyani zomwe Iye ananena kwa Abrahamu. Tsopano, Iye ndi mlendo, asanayambe wakhalapo uko kale. Iye anati, “Abrahamu, ali kuti mkazi wako, Sarah?”

<sup>240</sup> Kodi Iye anadziwa bwanji kuti iye anali ndi mkazi? Ndipo Iye anadziwa bwanji kuti dzina lake linali Sarah? Tsopano, Baibulo limanena kuti Abrahamu anamuza Iye kuti iye anali mu hema, kumbuyo kwa Iye; mu hema, kumbuyo kwa Iye.

<sup>241</sup> Iye anati, “Abrahamu, ine ndidzakuchezera iwe molingana ndi nthawi ya moyo, poti ine ndinakulonjeza iwe mwana uyu. Ine ndidzakupatsa iwe iye.” Ndipo Sarah, osati momveka, koma anaseka kwa iyemwini.

<sup>242</sup> Ndipo Mngelo, ali ndi nsana Wake ku hema, anati, “Chifukwa chiani Sarah waseka?” Mukuona izo? Yesu ananena kuti izo zikanadzachitika pakati pa Amitundu, isanafike

basi nthawi yotsiriza, Mesiya akanati adze pansipa mwa mawonekedwe a Mzimu Woyera.

243 Kodi chinthu choyamba chimene Mesiya anachiyamba kuchichita ndi chiani pamene Iye anabatizidwa ku Yordani, ndi Mzimu Woyera, kodi Iye anachita chiani? Anayamba kuchiritsa odwala.

244 Kodi chizindikiro Chake chotsiriza chinali chiani, ndi chizindikiro Chake Iye asanatembenuke kuchoka kwa iwo? Chizindikiro chija apo pomwe.

245 Kodi chitsitsimutso cha chipentekoste chinabweretsa chiani? Kuchiritsa odwala, zozizwitsa ndi zizindikiro.

246 Chizindikiro chotsiriza ndi chiani? Ndi ichi pano. Ndi angati kunja uko akudwala ndipo alibe khadi la pemphero? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Mukhale ndi chikhulupiriro ndi kumakhulupirira. Winawake akuti, “Ndiye bwanji apo, M’bale Branham?” Mzimu wa Mulungu umenewo, Ujayu Yemwe amapanga lonjezo, sangakhoze kulephera ndi lonjezo. Inu opanda makadi a pemphero, ine ndikutembenezira nsana wanga kwa inu. Inu muzipemphera. Ndipo ngati Mulungu ali Mulungu, ngati yankho Lake liri lowona, ndipo ine ndakuuzani inu Choonadi kudutsa mu masabata awa, kuti ichi ndi chizindikiro cha kuwonekera Kwake kwa posachedwa.

247 Malingaliro otukuka aliwonse, abwinobwino akudziwa kuti ife tiri pa mapeto a chinachake. Chitukuko sichingakhoze kuima motalikiranso. Ilo likungolukana ndi kugwedezeke. Nchiani chomwe likuyembekezera? Ntha—nthawi yake yapitirira motalika kwambiri. “Monga momwe zinali mu masiku a Nowa,” kupirira motalika. Izo zalowerera mu nthawi yowonjezera, chifukwa cha Osankhidwa. Izo zapitirira kale, koma Mulungu akuyembekeza kuti awutengere Mpingo Wake mu dongosolo. Iye akuyembekezera pa inu ndi ine.

Iye atapereka dalitsolo. Inu muzipemphera.

248 Pamene mkazi anagwira mphonje ya chovala Chake. Ena a akazi inu kunja uko tsopano, mulole iyi ikhale ngati nkhani ya Baibulo. Ena a akazi inu omwe mukukhulupirira tsopano, ndipo mukukhulupirira kuti inu muli ndi chikhulupiriro chokwanira kuti mumukhulupirire nacho Mulungu, mukhulupirire kuti chirichonse chimene Mulungu wanena ndi choona. Ndipo panali mkazi wamng’ono yemwe anagwira mphonje ya chovala Chake. Ndipo pamene iye anagwira chovala Chakecho, Iye anatembenuka, anati, “Ndani wandigwira Ine? Ndani wandigwira Ine?”

249 Ndipo iwo onse anakana izo. Anati, “Chabwino, aliyense akukugwirani Inu.” Petro anamudzudzula Iye, anati, “Aliyense akukugwirani Inu. Inu mukuneneranji izo monga choncho?”

<sup>250</sup> Iye anati, “Koma ine ndazindikira kuti ine ndafooka.” Uko ndiko kumasulira kolondola. “Ukoma wachoka mwa Ine.” Ndipo *ukoma* ndi “mphamvu.” Ndi angati akudziwa zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] “Ukoma wachoka mwa Ine.”

<sup>251</sup> Ndipo Iye anayang’ana pozungulira, pa unyinjiwo, mpaka Iye anamupeza mkazi wamng’onooyo. Ndipo Iye anamuuza iye kuti kuwukha magazi kwake kwaleka, chifukwa chikhulupiriro chake chamuchiritsa iye. Ndi kulondola uko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

<sup>252</sup> Baibulo linanena, kuti, “Iye ali pakali pano Wansembe Wamkulu yemwe angakhoze kukhudzidwa ndi kumverera kwa zifooko zathu.” Kodi inu, atsopano, obwera mwatsopano, mukukhulupirira izo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

<sup>253</sup> Tsopano, kumbukirani, machiritso! Ngati Iye akanati akhale atama pano atavala suti iyi, yomwe Iye anandipatsa ine, Iye sakanakhoza kukuchizani inu. Ngati inu mukwabwera pano pa nsanja, “Ambuye, kodi Inu mungandichize ine?” inu mukudziwa zomwe Iye akanati anene kwa inu? “Ine ndinachita kale izo. Ine *ndinatunduzidwa* chifukwaeha zolakwa zanu. Ndi mikwingwirima Yanga inu *munachiritsidwa*.” Chipulumutso ndi machiritso ndi ntchito yotsirizidwa. Ndi chikhulupiriro chanu kuti muzivomereze izo.

<sup>254</sup> Tsopano, Iye akanati achite chinachake kuti atsimikizire kuti Iye anali Mesiya. Tsopano, zinthu izi sizikutsimikizira kuti ndine Mesiya aliyense. Ndine wochimwa wopulumutsidwa mwa chisomo. Ndipo ziribe kanthu kuchuluka kwa momwe Mulungu angamandidzozere ine, Iye ayenera kuti akudzozeni inu, aponso. Izo zizingamangogwira ntchito ndi ine ndekha. Izo zimatengera inu, kuti muzipangitse izo kugwira ntchito. Ziribe kanthu kuchuluka kwa Mzimu Woyera womwe ungafike pa ine, Iwo uyenera uzikhala uli pa inu, aponso. Koma ngati “Iye ali Wansembe Wamkulu yemwe angakhoze kukhudzidwa ndi kumverera kwa zifooko zathu,” ndipo Baibulo linati, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse,” ndiye Iye achita mofanana. Iye ali pano, mwa ife. Kodi inu mukukhulupirira izo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

Tsopano, aliyense, khalani pa malo panu, mukhale molemekeza, mukupemphera.

<sup>255</sup> Ndipo mulole Ambuye Mulungu apereke izo. Basi, Ambuye, chonde. Anthu okondeka awa...ine ndiri...Ambuye, Inu mukudziwa cholinga changa chakukhala ndiri pano. Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu muwalole iwo kuti achiwone, ngati iwo sadzatero konse kachiwiri, muwalole iwo adziwe kuti Kudza kwa Ambuye kuli pafupi. Muwalole iwo adziwe kuti Mauthenga ankhanza awa, mwakuwoneka, awakondoweze iwo, osati kuti azichita mochenjera, osati kuti zikhale mwanga...mwa

ndekha. Koma chifukwa Inu mwaudzoza iwo, ndipo mwanena choncho. Tsimikizirani izo, Ambuye. Ine ndakuyankhulirani Inu. Ndiyankhulireni ine, Ambuye, kuti mawu anga ali owona, chifukwa iwo akuchokera kwa Inu. Ine ndikupempha mu Dzina la Yesu. Amen.

Landirani kuitana kwanu. Musaliphonye tsiku lanu.

<sup>256</sup> Ndi angati mu mzere wa pemphero uwu ali alendo kwa ine? Kwezani mmwamba manja anu, nonse inu omwe muli alendo. Nonse inu omwe muli kunjja uko, alendo, kwezani mmwamba manja anu.

<sup>257</sup> Ine sindikumudziwa munthu kupatula Gene Goad wakhala apayu, Pat Tyler ali apoyo. Ndi okhawo omwe ine ndikuwawona. Mwana wanga waima kumbuyo ukoyo, ndi okhawo omwe ine ndikuwadziwa.

<sup>258</sup> Mkazi uyo wakhala apoyo akusisita maso ake, atavala chipewa chofiira, wakhala apoyo. Kodi inu mukukhulupirira kuti Yesu anakumvani inu pamene inu munamupempha Iye kuti achize kupweteka kwa mutu wa chimfine uko? Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye anakumvani inu? Inu munali kupempherera izo, sichoncho inu? Ngati uko kuli kulondola, imirirani pa mapazi anu. Ngati icho chiri Choonadi, kwezani dzanja lanu. Ngati ine sindikukudziwani inu, ndipo inu simukundidziwa ine, kwezani dzanja linalo, manja onsewo. [Mlango akuti, “Ine ndinakuwonanipo inu kale.”—Mkonzi.] Amami? [“Ine ndakhalapo mu zitsitsimutso, kale.”] Inu munakhalapo mu zitsitsimutso zanga, kale. Koma, ine ndikutanthauza, ine sindikukudziwani inu. [“Ayi.”] Ayi. Chabwino. Chabwino. Tsopano izo zasiya. Inu mukhoza kupita kwanu ndi kukakhala bwino.

<sup>259</sup> Ine ndikufuna kuti ndikufunsemi inu anthu chinachake. Kodi mkazi uyo anakhudza chiani? Dzanja langa ndi ili, ine sindikukumbukira konse za . . . Iye wakhala ali mu misonkhano. Tsopano inu mukanati, “Nanga bwanji winawake mmwamba umo mu khondelo, pansu *kuno*, mwinamwake anali mu msonkhano nthawiyina kale?” Ine sindikanadziwa nkomwe yemwe inu munali. Chinthu chokha chimene ine ndikuchidziwa, nkuti inu mwangokhala . . . inu munali kuno mu msonkhano. Ndipo ndi uyo apo. Iye anakhudza Chinachake. Ndi chiani ana . . .

<sup>260</sup> Ine ndinati, kanthawi kapitako, Lawi la Moto lija. Kodi inu simukuliwona Ilo? Ndi angati ali nacho chithunzi cha Ilo tsopano? Iwo ali nacho icho muno mu msonkhanowu. Tsopano, Ilo likuwoneka ngati Lawi la Moto. Si choncho? Ndipo tsopano, moyo wa Ilo, kodi Ilo limabala chiani? Zofanana. Osati ine, tsopano. Ilo, kodi Ilo limabala chiani? Ntchito zofanana zomwe Ilo linkachita pamene Ilo linali mwa Mwana wa Mulungu.



Tsopano Ilo liri mwa ana aamuna ndi aakazi okhazikitsidwa, mwa chisomo cha Mwana woona wa Mulungu.

<sup>261</sup> Pomwe apo, bwana. Inu mukufuna kuthana nalo vuto la mtima ilo? Mukukhulupirira kuti Mulungu akupangani kukhala bwino, mutakhala apo pomwe? Inu munali kuyang'ana, mukudabwa, ndipo zonse mwakamodzi kumverera kwakung'ono kwachirendo kunafika pa inu. Ndiko kulondola. Ine sindikukudziwani inu. Ndikukudziwani ine? Inu simukundidziwa ine ndipo ine sindikukudziwani inu. Ngati uko kuli kulondola, kwezani mmwamba dzanja lanu. Inu mukukhulupirira vuto lanu la mtima latha? Gwedeze dzanja lanu. Chabwino, ndiye latha. Mwaona?

Inu mukukhulupirira? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

<sup>262</sup> Apa pali dona wakhala cha komwe kuno *apa*. Kodi inu simukukuwona Kuwala uko pa mkazi ameneyo? Iye ali ndi vuto la kapamba. Iye achiphonya icho. (Mulungu, muthandizeni.) Mtsikana wa a Small, kodi inu mukukhulupirira Mulungu akuchizani inu ku vuto la kapamba ilo? [Mlongo akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndiye imani pa mapazi anu. Inu munali ndi chikhulupiriro chochuluka kuposa momwe inu mumaganizira kuti munali nacho. Ine sindikumudziwa mkaziyo. Ichu chinali chisomo cha Mulungu. Ngati ife tiri alendo, gwedeze manja anu monga *chonchi*, dona. Apo. Ine sindikukudziwani inu. Koma chimene Iye wakuuzani inu, kodi icho ndi Choonadi, (kwezani mmwamba dzanja lanu), chimene Iye wanena? Chabwino. Ndiye khalani ndi chikhulupiriro, ndipo pitani kwanu ndi kukakhala bwino.

Ngati inu mungakhoze kukhulupirira!

<sup>263</sup> Dona uyu wakhala apayu, yemwe ali ndi vuto la mmimba, mmimba. Inde, Effie, ndi yemwe ine ndikuyankhula naye. Imirira, Effie. Kodi ilo linali vuto lako? [Mlongoyo akuti, “Zoono.”—Mkonzi.] Ine sindikukudziwa iwe. Ngati izo ziri zoono, kweza mmwamba manja ako. Ine sindinayambe ndakuwonapo iwe mu moyo wanga. Mulungu Kumwamba akudziwa zimenezo. Pita kwanu. Izo zatha. Mulungu akudalitse iwe.

<sup>264</sup> Ngati inu mufa mu machimo anu, ilo silikhala vuto la Mulungu. Inu mukhoza kukhala nthawizonse omvera kwambiri kwa mpingo, koma wochimwa ndi wosakhulupirira. Khalani nacho chikhulupiriro mwa Mulungu. Chabwino.

<sup>265</sup> Tsopano, anthu awa pano, uwu ndi mzere wa pemphero, kuika manja pa odwala. Kodi inu mukhulupirira izo, mulimonse? Tsopano, awo ndi anthu opanda khadi la pemphero, komwe kuli mzere wozindikira za mumtima, kunja uko opanda khadi la pemphero. Tsopano, ena nonse inu yambani kukhulupirira.

266 Musamayendeyende. Mwaona? Aliyense wa inu ndi mzimu. Mwaona? Aliyense wa inu ndi mzimu. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Mukanati musakhale, inu mukanakhala mutafa. Kotero, ndi mzimu wanu womwe ine ndikuwukamba, osati inuyo. Ndi mzimu wanuwo.

267 Bwerani kuno, dona. Kodi inu mukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito wa Mulungu? [Mlongo akuti, “Inde, bwana.”—Mkonzi.] Ndifefe alendo kwa wina ndi mzake. [“Inde, bwana.”] Ife sitikudziwana wina ndi mzake. Ngati uko kuli kulondola, kuti omvetsera, mkhonde mmwambamo, amvetse, ingokwezani mmwamba dzanja lanu, ngati ife tiri alendo, sitinayambe takomanapo. Mawonekedwe ake ndi awa. Pokhala kuti woyamba mu mzere anali mkazi, apa pali Yohane Woyera 4, mwamuna ndi mkazi, kukomana, nthawi woyamba mu moyo. Ngati uwu uli Mzimu wa Khristu pano pakati pa ife, ndiye Iye achita ntchito za Khristu.

268 Chonde musamasunthe. Tsopano, inu mumangowononga— a...I—inu mumawapweteketsa ena. Mwaona? Ine ndiri nawo ulamuliro pa aliyense wa inu. Ine ndikuyesera kuti ndikuthandizeni inu. Khalani chete kwenikweni ndi molemekeza. Chabwino.

269 Ngati Ambuye Mulungu ati andiuzi ine chinachake za inu...Ngati ine ndikanabwera kuno...Mwinamwake inu mukudwala. Inu mukhoza kusakhala muli, koma n—ngati inu muli, ndipo ine nditabwera kuno ndi kudzangoika manja anga pa inu, ndikuti, “Inu mukakhala bwino, dona,” inu mungazikhulupirire izo. Chifukwa, n—ndi zooni. Koma ngati Mzimu Woyera ukanaima pano ndi . . .

270 Bwanji nga—ngati uyu akanakhala Ambuye Yesu atavala suti iyi, ataima pano, ndipo inu ndikuti, “Ndichizeni ine. Ndichizeni ine, Ambuye”? Iye akanati, “Ine ndinazichita kale izo.” Koma Iye akanachita chinachake monga chimene Iye anachita pamene anali komwe kuno kalelo, monga Iye anachitira ndi mkazi pa chitsime, kuti akudziwitseni inu kuti ndi Iyeyo. Kodi Iye anamupangitsa chotani kuti iye adziwe? Pa kumuuzi iye chinachake chomwe chinali mu moyo wake. Ndi kulondola uko, omvetsera? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Nonse inu obwera mwatsopano? Iye anakhoza kumuuzi chinachake chimene chinali mu moyo wake.

271 Tsopano ngati Iye ati akuuzeni chinachake chimene chiri mu moyo wanu, monga Iye anachitira kwa Simoni Petro, kapena monga Iye anachitira kwa winawake mu Baibulo, momwe Iye ankachitira, ndiye izo zikanakupatsani inu chikhulupiriro chochulukira.

272 Kodi izo zikanamupatsa wina aliyense wa inu chikhulupiriro, kuti mukhulupirire? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

273 Tsopano, ndi izi apa, chabwino, osati kuseri kwa makatani ena akuda, osati malubwelubwe ena a mdierekezi, koma pomwe pano pa nsanja ndi inu, kuchokera mu Mawu a Baibulo. Izo zikhoza kukhala zosokonezeka pang'ono mu fioloje, koma ndi Lemba chimodzimodzi basi. Mwaona?

274 Ngati ine ndikanakhoza kukuthandizani inu, ndipo ine ndikanati ndisatero, ine ndikanakhala wonamizira. Ine sindikanakhala woyenera kuti ndiyime pano pambali pa Baibulo ili, ngati ine ndikanakhoza kukuthandizani inu ndipo nkusatero. Ine sindingakhoze kukuthandizani inu. Chinthu chokha chimene ine ndingakhoze kuchita ndi kukupangitsani inu kuti muzindikire chinachake, kuti Khristu ali pano kuti akuchizeni inu, akupangitseni inu kuchira ngati inu mukudwala.

275 Inu mukudwala. Inu mukuvutitsidwa ndi vuto lachidona. Ilo ndi vuto lachikazi. [Mlongo akuti, “Inde.”—Mkonzi.] Ndiko kulondola. Ngati uko kuli kulondola, kwezani mmwamba dzanja lanu.

276 Koteri kuti inu musati. . . inu mudziwe kuti ine sindikupeka ayi. Miniti yokha. Ikani chinachake pa mtima wanu, ndipo musingopemphera kwa nokha, mu mtima mwanu, pa chirichonse chimene inu mukufuna kuti Mulungu achite. Eya. Inu muli ndi chinachake pa mtima panu pakali pano? Ndi amuna anu. [Mlongo akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndi amuna anu. Inu mukukhulupirira Mulungu akhoza kundiuza ine chomwe chiri chovuta ndi iye? [“Inde, bwana.”] Ndi chinachake chalakwika ndi ubongo. [“Inde, bwana.”] Izo zimatchedwa, ngati kuuma kwa msempha mu ubongo. [“Inde, bwana.”] Izo ndi zoonu. [“Ndi chomwe izo ziri.”] Uko nkulondola. Ngati Mulungu ati andiuze ine yemwe inu muli, kodi izo zikupangitsani inu kukhala ndi chikhulupiriro chochulukuka? Inu mukukhulupirira izo, ndi mtima wanu wonse? [“Inde, bwana.”] Nancy Gillespie, pitani kwanu, Yesu Khristu wakuchiritsani inu ndi mwamuna wanu, ndipo akupangitsani inu kuchira. [“O, Aleluya!”] Tengerani mpango umenewo kwa iye. Izo ndi zoonu. Sichoncho izo? [“Inde.”] Chabwino. Pitani pa ulendo wanu.

277 Tsopano kodi inu mukumukhulupirira Mulungu? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Ingokhalani ndi chikhulupiriro. Musati muzikaikira.

278 Tsopano ine ndiwufunsa mpingo waukulu uwu pano ngati inu mungapemphere ndi ine chifukwa cha anthu awa. Awo ndi amayi a winawake, bambo a winawake, wokoma mtima a winawake, mwamuna wa winawake. Pempherani.

279 Musayendeyende, chonde. Inu basi. . . Inu mukungousokoneza msonkhanowu. Khalani bata kwenikweni ndi kumapemphera. Ife tibalalitsidwa mu maminiti teni ngati muti mungokhala—ingokhalani molemekeza.

280 Bwerani, dona. Ngati ine sindinena mawu amodzi, nkungokupemphererani inu, inu mukhulupirira izo?

Ambuye Yesu, ine ndikupemphera kuti Inu mumuchiritse iye, mu Dzina la Yesu.

Bwerani, m'bale wanga. Khulupirirani ndi mtima wanu wonse.

281 Atate athu Akumwamba, mu Dzina la Yesu Khristu mupangitseni iye kuchira. Amen.

282 Mulungu akudalitseni inu, m'bale wanga. [M'bale akuti, "Akazi anga ali pano, ali nazo zochuluka...?..."—Mkonzi.] Chabwino, bwana, inu bwerani. Izo sizipangitsa kusi yana kulikonse, bwana. Ayi. Zonse ziri bwino. Ine ndikudziwa chomwe chavuta ndi inu, koma palibe chifukwa choti ndikuuzireni inu. Kodi inu mukuganiza, izo zingakuthandizeni inu ngati ine nditakuuzani inu? ["Ayi."] Sizingakuthandizeni inu. Ndithudi. Koma, mulimonse, vuto lanu la mtima linakusiyani inu pamene inu mumachoka apo. Koteri zingopitani pa njira yanu, mukusangalala, muzinena kuti "Zikomo Inu, Atate."

Bwerani, bwana.

283 Mu Dzina la Ambuye Yesu, Atate, ine ndikupemphera kuti Inu mumuchiritse iye. Amen.

Khulupirirani tsopano.

284 Khalani ndi chikhulupiriro tsopano, mlongo. Bwerani, monga onse awa . . . Penyani, alipo pafupi anthu firii sauzande pano omwe akukupemphererani inu tsopano.

Mu Dzina la Yesu, mulole iye kuti achiritsidwe. Perekani izo, Atate.

285 Bwerani. Bwana, nyamakazi idzakupezani inu, tsiku lina, ngati inu simukhala ndi chikhulupiriro pano. Inu mukhulupirira izi pano? Ndiye pitani ndi kukachiritsidwa, mu Dzina la Yesu Khristu.

Bwerani, mlongo.

286 Atate Mulungu, mu Dzina la Ambuye Yesu, mchiritseni mlongo wathu. Amen.

Bwerani, mukhulupirira tsopano.

Aliyense azikhulupirira ndi kumapemphera.

287 Atate Akumwamba, ine ndikupemphera kuti Inu mumuchiritse iye, mu Dzina la Yesu. Amen.

288 Bwerani. Tsopano, m'bale, ngati ife tikanakhala nawo masomphenya kwa aliyense, izo zikanangoti basi . . . inu . . . Iwo bwenzi atachita kundinyamula ine pochoka pa nsanja; mwaona, ine bwenzi nditapita pansu. Koma kuti inu mukhoze, kudziwa, pitani ndi kukadya chakudya chanu usikuuno. Icho chikakoma

bwino kwenikweni. Vuto la mmimba lakusiyani inu. Mwaona? Pitani ndi kukadya. Chabwino.

Bwerani, mlongo.

<sup>289</sup> Ine ndimachita izo kwa cholinga, kudziponyera ndekha kumbali, abwenzi. Chifukwa, masomphenya. . . Ndi angati akudziswa kuti Yesu anati, “Ukoma wachoka mwa Ine”? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Ine ndiri, pakali pano, ine ndangokhala wofooka, kwenikweni.

<sup>290</sup> O Atate, ine ndikupemphera kuti Inu mumuchiritse mlongo wathu. Mu Dzina la Yesu, perekani izi.

<sup>291</sup> Bwerani, mlongo wokonedwa. Musati mukaikire tsopano. Bwerani, mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse.

<sup>292</sup> O Ambuye, mu Dzina la Khristu, muchizeni mlongo wathu. Mupatseni iye chigonjetso chake, Ambuye.

<sup>293</sup> Bwerani, mlongo wanga. Baibulo linati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.”

Mu Dzina la Yesu, mulole iye kuti achiritsidwe. Ameni. Perekani izi.

<sup>294</sup> Bwerani, mlongo. Vuto lanu la nsana lakusiyani inu, kotero inu mukhoza kupitirira pa njira yanu, mukusangalala.

<sup>295</sup> Kodi inu mukukhulupirira? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Mwaona? Bwanji, bwanji? Mvetserani. Ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu. Mvetserani, abwenzi. Pamene anthu awo akubwera pano. . . Baibulo, Ilo limati, “Iwo azidzaika manja pa odwala, ndipo iwo azidzachira,” ndi zochuluka basi ngati kuwauza iwo. Kodi inu simukukhulupirira Izo? [“Ameni.”] Ndithudi, inu mukukhulupirira.

<sup>296</sup> Tayang’anani kuno, bwana. Inu mukundikhulupirira ine kuti ndi wantchito wa Iye? Tsopano, pali mkazi yemwe ndinamumitsa kanthawi kapitako; ndinu mwamuna wake. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiuza ine mavuto anu? [M’bale akuti, “Inde, bwana.”—Mkonzi.] N—ndi kukupangitsani inu kuchira? [“Ine ndiri ndi pafupi zinthu zinai kapena zisanu zosiyana pano.”] Inde, bwana. Chabwino, inu, vuto lanu la mmimba ndi chinthu chimodzi chimene chikukuvutitsani inu, pang’ono. Ndiko kulondola. Inde, bwana. Inde, bwana. Ndi mwera wanu. [“Ndiko kulondola.”] Inde, bwana. Chifukwa, mwera wanu ndi womwe umakupangitsani inu manjenje, ndi zomwe zimakukwiyitsani inu. Ndizo ndendende kulondola. Inu mukuganiza akazi anu akhoza kukhala bwino, nawonso, ngati inu mungakhulupirire? Chabwino. Ngati inu muti mukhulupirire ndi mtima wanu wonse, ndiye akazi anu akhoza kuchiritsidwa. [“Iwo akudwala.”] Eya. Manjenje, ndi kusokonezeka, ndi kufooka, ndi zinthu. Inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse tsopano, iwo achiritsidwa? Pitirirani pa njira yanu ndi kumati, “Zikomo

Inu, Ambuye Yesu wokonedwa,” ndipo iwo akhala bwino, nawonso.

<sup>297</sup> Ambuye Yesu, ine ndikupemphera kuti Inu mutithandize izi, O Ambuye, ndi kuchipanga icho motero kuti chake. . . Ulemerero wa Mulungu ubwere pa iye, ndipo iye achiritsidwe. Mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

<sup>298</sup> [M’bale akuyamba kuyankhula mu lirime lina—Mkonzi.] Tsopano pitani, mukukhulupirira, Bambo Dodd, ndi kukhulupirira ndi mtima wanu wonse, ndipo mukakhala bwino. Chabwino.

Bwerani, bwana.

<sup>299</sup> Atate Akumwamba, ine ndikupemphera kuti Inu mumuchize m’bale wathu ndi kumupanga iye kukhala bwino, mu Dzina la Yesu.

Bwerani, mlongo, kuno. Mukhulupirireni Iye ndi mtima wanu wonse tsopano.

<sup>300</sup> O Mulungu, Atate athu, ine ndikupemphera kuti Inu mumupange iye kukhala bwino, mu Dzina la Yesu.

<sup>301</sup> Bwerani, m’bale, mbweretseni mwanayo. Musakaikire tsopano. Ingomubweretsani iye mpaka kuno, ngati kuti mukubwera pansu pa mtanda.

Ambuye, ine ndikuwadalitsa iwo mu Dzina la Yesu. Amen.

Bwerani, mlongo. Bwerani, mukukhulupirira tsopano ndi mtima wanu wonse.

Atate, mu Dzina la Yesu, ine ndikupemphera kuti Inu mumuchize iye. Amen.

<sup>302</sup> Khulupirirani tsopano ndipo mukhale molemekeza kwenikweni. Khulupirirani ndi mtima wanu wonse.

<sup>303</sup> Mu Dzina la Ambuye Yesu, mulole iye achiritsidwe, Ambuye. Amen.

<sup>304</sup> Bwerani, mlongo, khulupirirani ndi mtima wanu wonse. Khulupirirani kuti iye akhala bwino tsopano ndipo alandira kupenya kwake ndi zonse.

<sup>305</sup> O Ambuye, ine ndikupemphera kuti Inu mumuchize iye, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

<sup>306</sup> Usiku wina, ndikupempherera mnyamata wamng’ono, wa pafupi usinkhu wa zaka fifitini, sikisitini. Iye ankadutsa apo, munthu wamng’ono; wa chikhulupiriro chachikulu. Ine ndinayang’ana pa iye. Ine ndinati, “Zona, iwe ukudziwa, mwana.” Ndipo—ndipo kotero iye anapitirira kutuluka, anayenda akutsika pamenepo. Ndipo mnyamata wamng’ono, anabadwa ali wakhungu, analandira kupenya kwake, ndipo anafuulanso, “O, M’bale Branham, ine ndikukhoza kupenya.”

307 Pano pali, muno, chingwe chochokera kwa mwana, mwana wa mutu wa liombo. Wanyalirapo mochuluka *chotero*, mu usiku umodzi, pakungodutsa apa. Zinthu zikuchitika. Inu muyenera kuti muzikhulupirira, apabe. Mwaona? Inu sindinu nkhuu. Ndinu mphungu.

Bwerani.

308 Mu Dzina la Yesu, Ambuye, mulole iye achiritsidwe kwa ulemerero wa Mulungu. Amen.

Bwerani, mukukhulupirira, muli ndi chikhulupiriro.

309 Inu mukudziwa, chinthu china chimzake . . . Inu mukudziwa chimene ine ndikuganiza, abwenzi? I, ine sindiri, ine sindiri kuwazazira anthu, koma ine ndikufuna kuti inu mudziwe chinthu chimodzi. Ife tiri ndi televizioni mochuluka kwambiri mu miyoyo yathu. Ife timafuna zosangalatsa. Ife sitiri . . . Mulungu sali kusonyeza zinthu izi kuti azikusangalatsani inu. Iye akufuna kuti inu muzindikire Kukhalapo Kwake. Zinthu zimenezo zikhoza kuchitika kwa aliyense, koma izo zikhoza pafupifupi kukupha; o, ine sindingakhoze kuutsiriza mzere.

310 Apa, bwerani pano, dona. Inu ndi ine ndife alendo kwa wina ndi mzake. Inu mukuganiza kuti Mulungu akhoza kundiuza ine lomwe liri vuto lanu? [Mlongo akuti, “A-nha.”—Mkonzi.] K—kodi zingakuthandizeni inu?

311 Kodi izo zingakuthandizeni inu nonse n—ngati Mulungu akananena chinachake tsopano kwa mkazi uyu?

312 Ndi khutu lanu. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akupangitsani inu kuchira? [Mlongo akuti, “Chabwino, zikomo Mulungu! Inde.”—Mkonzi.] Inu mukuwopsyezedwa kuti ndi khansa. Ndipo iyo ili mu khutu lanu lakumanzere. Ndi kulondola uko. [“Ndiko kulondola.”] Chabwino, iyo inali, koma iyo siili tsopano. Tsopano, penyani. Kodi inu mukumukhulupirira Mulungu? [“Ine ndikutero.”] Ngati Mulungu ati andiuze ine yemwe inu muli, kodi izo zikuthandizani inu? Chabwino, Ruby Thompson, pita kwanu ndipo ukakhale bwino, mu Dzina la Yesu Khristu. Mwaona? Khalani ndi chikhulupiriro.

313 Bwerani tsopano. Musati mukaikire. Mulungu akhoza kundiuza ine vuto lanu. Kodi inu mukuganiza kuti izo zingakuthandizeni inu? [Mlongo akuti, “Inde.”—Mkonzi.] Ndiye, matenda a shuga. [“Inde.”] Vuto la mtima. Zipitani pa ulendo wanu ndipo mukakhale bwino, ndipo zikhulupirirani Mulungu. [“...?...”] Inde. [“...?...”] Ndi usinkhu wa ukalamba basi umene ukubwera pa inu. Tsopano, muzingopita, mukukhulupirira.

314 O Ambuye, ine ndikupemphera kuti Inu mumuchize m’bale wathu ndi kumupangitsa iye kuchira. Amen. Mulungu, perekani izi.

Bwerani, mlongo wokondedwa.

Mu Dzina la Ambuye Yesu, mulole iye achiritsidwe. Amen.

Kupempha madalitso a Mulungu, zingakhoze kulephera bwanji izo?

Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole izo zikhale, Ambuye. Amen.

Bwerani, m'bale wanga.

<sup>315</sup> Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole m'bale wathu achiritsidwe. Amen.

<sup>316</sup> Bwerani, m'bale wokondedwa. Mulungu akudalitseni inu. Abweretseni amayiwo. Kazibwerani, mlongo.

Mu Dzina la Yesu Khristu, inu mutachiritsidwa.

Bwerani.

Mu Dzina la Yesu Khristu, mlongo wathu atachiritsidwa tsopano.

<sup>317</sup> Eya. Zikhulupirirani tsopano. Chinthu chomwecho chichitika muli panso apo, ngati inu simukaikira.

<sup>318</sup> O Mulungu, mdalitseni wosauka uyu, m'bale wokondedwa. Ine ndikupemphera, Atate Akumwamba, kuti Inu mumuchize iye ndi kumupanga iye kukhala bwino. Ndipo mulole izo zifike pochitika kuti iye alandire kupenya kwake ndi kupangitsidwa kukhala bwino, mu Dzina la Yesu. Amen.

<sup>319</sup> Khalani ndi chikhulupiriro tsopano. Musakaikire. Ine sindingakhoze kuchiza. Iye ali pano basi. Iye ndi mchiritsi. Musati mukaikire. Mukhale ngati Bartimeo wakhungu, musingoyang'anira manja anu.

<sup>320</sup> Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole mlongo uyu achiritsidwe. Chabwino.

Bwerani, mlongo, wokondedwa.

Kodi inu mukukhulupirira, aliyense? Kwenikweni . . .

<sup>321</sup> Chinachake chinachitika. Miniti chabe. Munthu uyo yemwe wakhala apo, inu muli ndi mphumu, bwana. Uko nkulondola. Inu munali kupemphera. Inu munapotoloka, kuti munene, "Kodi izo si zodabwitsa?" Ine ndikuuzani inu chinthu china. Iwo anatenga pafupi magawo awiri a utatu wa mimba yanu, chifukwa cha vuto la mmimba. Uko nkulondola. Sichoncho izo? Ngati uko kuli kulondola, gwedezani dzanja lanu. Ndipo ndife alendo kwa wina ndi mzake. Yesu Khristu anakuchizani inu. Chikhulupiriro chanu chinakupangitsani inu kuchira. Pitani pa ulendo wanu, mukusangalala.

O, musakaikire. Khulupirirani.

<sup>322</sup> Chabwino, dona. Inu dikirani miniti. Tsopano, inu simuli pano kwa inu eni. [Mlongo akuti, "Ayi."—Mkonzi.] Inu muli pano chifukwa cha wina wake. ["Inde."] Ndiko kulondola. Ndipo m'bale wanu sali kuno. ["Ayi."] M'bale wanu sali ngakhale mu



dziko lino. ["Ayi."] Iye ali ku St. Louis. ["Ndiko kulondola."] Iye ali mu chipatala. ["Ameni."] Iye ali ndi vuto la mtima. ["Ndiko kulondola."] Ndipo iye ali, wakhala ali mtumiki. ["Ameni."] Ndipo inu mumaganiza kuti ngati ine ndikanadutsa ndi kuika manja pa inu, ["Ameni."] kuti inu...ine "sindimadziwa" zomwe ine ndinali kuzikamba. ["Ine ndimadziwa."] Koma ine ndimadziwa. Kotero, inu mupitirire pa njira yanu, ndipo iye akhala bwino, ine ndikukhulupirira. Chabwino. Khalani ndi chikhulupiriro. Zingopitirirani.

323 Pali mkazi wina muno, akuganiza chinthu chomwecho pakali pano, za mwana wamkazi yemwe anaphedwa. Akazi a Weatherman...Waterman, iwo ali. Akazi a Waterman, khulupirirani ndi mtima wanu wonse tsopano. Mwana wanu wamkazi anatengedwa pa cholinga. Musakaikire. Zimukhulupirirani Mulungu.

324 O Mulungu, mu Dzina la Yesu Khristu, mulole iye akhale—wochiritsidwa. Ameni.

Bwerani, mukukhulupirira tsopano ndi mtima wanu wonse.

325 O Ambuye Mulungu, Mlengi wa miyamba ndi dziko lapansi, mupereke machiritso kwa mkazi uyu, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

Zikhulupirirani tsopano.

326 Tsopano penyani. Palibe machiritso a udokotala. [Mlengo akuti, "Ndiko kulondola."—Mkonzi.] Koma pali machiritso Akumwamba. ["Ndiko kulondola."] Ndiko kulondola. Inu mukukhulupirira izo? ["Zedi."] Iye akhala bwino bwino ndi kuchira. ["Inde. Uko nkulondola."]

327 Themberero, ine ndikumutemberera mdierekezi uyu yemwe wachita choipa kwa mwana uyu. Ndipo ine ndikulichotsa themberero ili pa iye, mu Dzina la Yesu Khristu. Mulole iye akhale mwana wabwinobwino. Ameni.

Izo ziyenera kukhala choncho. Chabwino.

Zipitirirani, mukusangalala. Khalani bwino ndipo mukadye chakudya chanu. Chabwino.

Bwerani, bwana. Mukhulupirireni Iye, ndi mtima wanu wonse.

Mu Dzina la Ambuye Yesu, iye atachiritsidwa. Ameni.

328 Izo zakhudza malo ochuluka kwambiri mwa omvetsera! Miniti yokha. Izo, ndi angati muno omwe ali ndi manjenje a mmimba, mulimonse? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Iwo ndi ochuluka kwambiri, ine sindingathe... Mukuwaona pamenepo? Aliyense wa inu, ali ndi manjenje a mmimba, imirirani pa mapazi anu. Pano pali njira yomwe mungazichotsere izo. Imirirani pa mapazi anu, miniti yokha.

Imani njii, bwana. Pitani, mukukhulupirira, m'bale wanga.

Mu Dzina la Yesu Khristu, inu mutachiritsidwa.

329 Bwerani tsopano. Mukhulupirire ndi mtima wanu wonse. Inu mukukhulupirira, mlongo? Mu Dzina la Yesu Khristu, inu mutachiritsidwa.

330 Manjenje, nthawizonse zakhala ziri, moyo wanu wonse. [M'bale akuti, "Ndiko kulondola."—Mkonzi.]

331 Aliyense yemwe akuvutitsidwa ndi vuto la manjenje, ndi impsyo, imani pa mapazi anu. Imirirani pa mapazi anu, aliyense yemwe ali nalo ilo.

332 Pitani, mukukhulupirira tsopano. Mukhale ndi chikhulupiriro. Mwaona? Imirirani pansi *apo* pomwe.

333 O Ambuye Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu muchitire chifundo pa m'bale wathu, ndipo mumupange iye kukhala bwino, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

Mukhale ndi chikhulupiriro. Inu mukukhulupirira tsopano, mlongo wokondedwa?

334 Mu Dzina la Ambuye Yesu, mulole iye achiritsidwe, Atate, kwa ulemerero wa Mulungu.

Chinachake chikuchitika.

335 Kodi awo ndi onse ake, Billy? [M'bale Billy Paul Branham akuti, "Mutenge mmodzi wina."—Mkonzi.] Eya. Eya.

336 Bwerani kuno, bwana. Ife ndi alendo kwa wina ndi mzake? [M'bale akuti, "Zedi."—Mkonzi.] Mulungu akutidziwa tonse ife, sichoncho Iye? ["Zedi."]

337 O, izo zikungochitika paliponse. Kumbukirani, alaliki, abale anga, abale anga mphungu zofunika, pamene ine ndichoka kuno, kwa masabata, inu mudzapeza osonkhana anu akuchitira umboni wa kuchiritsidwa. Iwo achiritsidwa, koma iwo sakudziwa izo. Mwaona? Mwaona? Izo zikungochitika paliponse. Bwanji ife sitimakhala ndi chikhulupiriro cha mtundu uwo pa kuyamba pomwe, abwenzi? Ichi ndicho.

338 Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kukuthandizani inu? Inu mukukhulupirira Mulungu akhoza kundiuza ine lomwe liri vuto lanu? [M'bale akuti, "Inde, bwana."—Mkonzi.] Inu muli ndi kupweteka mutu kwamphamvu. Inu mumakhala mukuchita chidima. Izo zimayambitsidwa ndi chophuka cha pa khosi. Ndiko kulondola. Inu mukukhulupirira Mulungu akudziwa yemwe inu muli? ["Inde ndikutero."] Ndinu mtumiki. ["Inde, bwana."] Dzina lanu ndi Rev. Jack Cole. ["Inde, bwana."] Ndizo ndendende kulondola. Pitani, mukukhulupirira, bwana.

339 Aliyense wa inu, amakhala ndi chizungulire kapena amakhala ndi kupweteka kwa mutu, imirirani pa mapazi anu. Munthu aliyense, ali wodwala, imirirani pa mapazi anu.

340 O, Mulungu! Nchiani chingachitike ngati izo zikanangotero! Nchiani chikanati chichitike! Kodi inu mukukhulupirira izo?

[Osonkhana akusangalala ndipo akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]  
Ndi angati okhulupirira ali pano, akhutitsidwa kuti chinthu ichi ndi Mzimu Woyera? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Ine sindingakhoze kumachita zinthu zimenezo. Kodi ndinu okhulupirira?

<sup>341</sup> Ikani manja anu pa wina ndi mzake ndipo mumufunse mdierekezi kuti amusiye munthuyo yemwe inu mwayikapo manja anu. Pemphero lanu liri chimodzimodzi monga langa. Ikanani manja anu, pa wina ndi mzake. Ndiko kulondola.

Dona, pamwamba *apo*, chifuwa chakusiyani inu apo.


<sup>342</sup> Vuto la mwera lakusiyani inu, m’bale. Inu mukhoza kutsitsa manja anu pansu ndi kumafuula matamando.

<sup>343</sup> TB, ili ndi dona wamng’ono uyo waima apoyo, iyo yachokapo. Uyiwale zimenezo. Yesu Khristu wakuchiritsani inu.

Izi ndizo, abwenzi. Tiyeni tizimupatsa Mulungu matamando.

O Ambuye, Inu muli pano.

<sup>344</sup> Ine ndikumutsutsa mdierekezi, mu ntchito zake zonse. Ine ndikuwutsutsa mzimu woipa uliwonse. Satana, iwe wayalutsidwa. Iwe wadzuzulidwa, mu Dzina la Yesu Khristu. Ine ndikukulamulira iwe, mwa Mulungu wamoyo, tuluka mwa omvetsera awa. Iwe sungakhoze kuwapanga iwo kukaikira, kenanso. Mzimu Woyera wadzipangitsa Wokha kukhala weniweni pamaso pa iwo. Iwe sungakhoze kuwapangitsa iwo kukaikira, kenanso. Iwo aikanana manja pa wina ndi mzake. Yesu anati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira: ngati iwo ayika manja awo pa odwala, iwo adzachira.” Satana, iwe walephera.

<sup>345</sup> Yesu, Inu mwawina. Inu ndinu Mulungu wa Kumwamba. Mulole mphamvu ya matenda ndi mphamvu ya Mdierekezi iswedwe, pa anthu awa, mu Dzina la Yesu Khristu. 

*MOMWE MPHUNGU IKASULIRA* CHA60-0403  
(As The Eagle Stirreth)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lamlungu madzulo, Epulo 3, 1960, ku Municipal Auditorium mu Tulsa, Oklahoma, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2015 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)